# Buku la Mphunzitsi

## Nthawiyabaibulo
## Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi

Maphunziro B7 - B12

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**
Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**
Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**
A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khrisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

    1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
    2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
    3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
    4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| MAPHUNZIRO A | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO B | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO C | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

## B7 – KALASI 3
**Phunziro Loyamba – Moyo wa Yosefe**
**Mutu – Azondi mu Aigupto**

**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 41: 46-57 ndi 42: 1-38***
**Vesi Yoloweza:** ***Numeri 32: 23***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Ife sitingachimwe ndi kukhala osalangidwa.
2. Ife tikuyenera kuvomereza tchimo lathu tisanakhululukidwe kuti tilandire chikhululukiro chimene ndi Ambuye Yesu yekha amene amapereka.

### MAWU OYAMBA

Fotokozerani ophunzira kuti Aaigupto ankadalira zokolola zawo kukhala zakudya ndipo zaka zisanu ndi ziwiri za njala inali nthawi yovuta kwambiri kwa anthuwa. Tirigu anali ofunika kwambiri nthawi imeneyo chifukwa ndiye chinali chakudya chawo cha tsiku ndi tsiku komanso ankasungika kwa nthawi yayitali. Komanso ankamugwiritsa ntchito ngati ndalama. Fotokozani kuti dziko la Aigupto silinkavutika kwambiri nthawi ya njala kuposa mayiko ena ozungulira chifukwa cha Mtsinje wa Nailo.

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Kunali njala zaka zisanu ndi ziwiri ***(vesi 54)*** ndipo ndi Yosefe yekha amene ankapereka zosowa za anthu ***(vesi 55)*** kuchokera pa tirigu wambiri amene anasunga m'nyumba zosungira za Farao.
2. Abale a Yosefe anabwera ku Aigupto kudzagula tirigu chifukwa cha njala. ***(42: 1-3)***
3. Yosefe anazindikira abale ake koma iwo sanamuzindikire. ***(42: 7)*** Iye anawayika m'ndende masiku atatu.
4. Yosefe anachita zinthu kwa abale ake ndi cholinga choti avomereze zoyipa zomwe anamuchitira. ***(42: 21)*** Iwo akatero ndi pamene akhoza kuyanjanitsidwa.
5. Maganizo awo ndi chikumbumtima chawo chinawatsimikizira kuti anali olakwa ndipo anamvetsa chifukwa chimene chinachititsa kuti akhale m'mavuto amene amadutsamo.
6. Ngakhale anamulakwira, Yosefe anawalirira ***(vesi 24)*** ndipo anawapatsa chakudya cha ulendo wawo pamene ankabwerera kwawo kwa abambo awo Yakobo, koma anasunga Simeoni m'ndende ndi kulamula kuti Benjamini, mwana wamng'ono, akabwere naye ku Aigupto.
7. Yakobo anadandaula kwambiri pamene anamufotokozera zonse zimene zinachitika ndipo anati sadzalola kuti Benjamini amutenge ndi kupita naye ku Aigupto. ***(42: 38)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**
**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Azondi mu Aigupto.

### KUKUMBUTSANA

Kambiranani ndi ophunzira momwe Vesi Yoloweza ikufotokozera phunziro lonse mwachidule.

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Onani kufunika kwa kutembenuka mtima ndi kutembenukira kwa Ambuye Yesu kuti atikhululukire.
2. Kufunika komvetsetsa ***1 Yohane 1: 9: "Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse."***
3. Onani Njira ya Chipulumutso: 1) Kuvomereza kuti ndinu wochimwa. 2) Kukhulupirira kuti Ambuye Yesu anafa m'malo mwanu pa mtanda. 3) Kuvomereza kuti Yesu ndi Ambuye a moyo wanu.

## B7 – KALASI 4
**Phunziro Loyamba – Moyo wa Yosefe**
**Mutu – Mayesero a chinyamata chake**

**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 39: 1-23 ndi 40: 1-23***
**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 39: 21***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Yosefe sanagonjere mayesero.
2. Ambuye anali ndi Yosefe mu ukapolo, m'mayesero ndi m'ndende. Yosefe anadalira ndi kumvera Ambuye.

### MAWU OYAMBA

Kumbutsani ophunzira pamene yafika nkhani kuchokera mu B6. Tsopano Yosefe anali mu Aigupto, koma mavuto ake sanathe. Mulungu akulola kuti adutse nyengo zovuta, kuti akonzekere ntchito yofunika kwambiri m'tsogolo. Kumbutsani ana kuti nthawi zina Mulungu amatiyesa polola kuti tidutse m'mayesero amene amalimbitsa ife kuti tikhale olimba m'tsogolo.

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Yosefe anayesetsa kukhala khalidwe labwino pamene anali kapolo mu Aigupto ndipo mosachedwa Potifara anamudalira. ***(39: 2)***
2. Mkazi wa Potifara anamunamizira Yosefe kuti ankafuna kumugwirira ndipo anaponyedwa m'ndende. ***(39: 11-20)*** Koma Yosefe anali mnyamata wangwiro amene anapitirira kudalira Mulungu, ngakhale anali mu nyengo zovuta. Mulungu anamudalitsa posintha nyengo zake ndi kupanga kuti akhale wolamulira zochitika m'ndende. ***(39: 21-23)***
3. Am'ndende awiri anali ndi maloto ndipo Yosefe anawamasulira. ***(40: 8)***
4. Tanthauzo la maloto a woperekera zakumwa unali uthenga wa moyo ndipo anamasulidwa m'ndende, koma tanthauzo la maloto a wophika buledi unali uthenga wa imfa, motero wophika buledi anaphedwa.
5. Yosefe anapempha woperekera zakumwa kuti akamukumbukire ndi kupempha Farao kuti amuthandize akamasulidwa koma iye anayiwala Yosefe. ***(40: 14 ndi 23)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**
**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Mayesero a chinyamata chake.

### KUKUMBUTSANA

Kambiranani ndi ophunzira momwe Vesi Yoloweza ikufotokozera phunziro mwachidule pokhudzana izi:
1. Moyo wa Yosefe m'nyumba ya Potifara; ndi
2. Moyo wa Yosefe m'ndende.

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Ife sitikuyenera kugonjera mayesero koma tikuyenera kupempha Ambuye tsiku ndi tsiku kuti azitithandiza kugonjetsa.
2. Chinsinsi chokhala mboni yopindula ya Ambuye ndi kuzindikira zomwe zikuchitika mwayi umene tili nawo kuti tithe kufotokoza za Ambuye Yesu pa zomwe ena zikuwachitikira, ndi cholinga chofuna kuwabweretsa kwa Mpulumutsi.
3. Onani Zowerenga Zoonjezera, ***Aefeso 6: 13-17*** ndi ***Yakobo 1: 12-18***, ndi kulingalira momwe tingagonjetsera mayesero m'miyoyo yathu.

## B7 – KALASI 3
**Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Yosefe**
**Mutu – Benjamini ndi nkhani yoyipa!**

**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 42: 35-38; 43: 11-14, 24-31; 44: 1-34***
**Vesi Yoloweza:** ***Aefeso 4: 32***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Yuda, amene anali pamodzi ndi abale ake kugulitsa Yosefe ku ukapolo, tsopano akudzipereka kuti akhale kapolo kuti apulumutse Benjamini. ***(44: 33)***
2. Mulungu angathe kugwira ntchito miyoyo yowuma ndi kuyisintha kwathunthu.

### MAWU OYAMBA
Kambiranani ndi ophunzira za momwe tchimo la abale a Yosefe linabweretsera mavuto pa miyoyo yawo komanso pa moyo wa abambo awo Yakobo. Fotokozani momwe tchimo lingabweretsere mavuto m'banja mwanu ndi pakati pa anzanu pamodzi ndi pa moyo wanunso.

### KUTSIRIZA
**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Njala inapitirira ndipo abale ake anapitanso ku Aigupto kukagula chakudya. Yakobo sankafuna kuti Benjamini apite ku Aigupto. ***(43: 11-13)*** Koma ndi Yosefe yekha amene akanatha kukwaniritsa zosowa zawo ndi kuthetsa mavuto awo.
2. Abale aja onse anayitanidwa ku nyumba ya Yosefe kuti akadye koma iwo sanamuzindikirebe. ***(43: 16)***
3. Abale amene anali ndi mantha aja anasangalala ndi chakudya chomwe Yosefe anawapatsa m'nyumba yake yaufumu. Yosefe akulira pamene waona mng'ono wake Benjamini. ***(43: 30)***
4. Iye akulamula kuti kapu yake yasiliva ayike m'thumba la Benjamini ndi kunena kuti Benjamini ndi amene waba ndipo ayenera kulangidwa. ***(44: 17)***
5. Nthawi yonseyi Yosefe akuyesa ndi kuona moyo wa abale ake ngati ali oyenera kuti awakhululukire, chomwe iye anali pafupi kuchita.

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**
**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Benjamini ndi nkhani yoyipa!

### KUKUMBUTSANA
Fotokozani kwa ophunzira kuti:
1. M'miyoyo yathu muli malo opanda kanthu mpaka pamene tavomereza machimo athu ndi kubwera kwa 'Yosefe wauzimu', Ambuye Yesu, kuti atikhululukire.
2. Phwando la madalitso likudikira amene akhululukidwa, dalitso lopita Kumwamba m'tsogolo.

### KHALANI MOYO UMENEWU
**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Dziwani kuti tchimo limabweretsa mavuto.
2. Pamene talapa ndi kuvomereza machimo athu Ambuye Yesu ndi wokonzeka kutikhululukira.
3. Pamene Ambuye Yesu atikhululukira, ifenso tikuyenera kukhululukira amene anatichimwira. ***(Aefeso 4: 32)***

## B7 – KALASI 4
**Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Yosefe**
**Mutu – Malo ake okwezedwa**

**Ndime Yowerenga:** ***Genesis 41: 1-45***
**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 41: 38***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Yosefe anakwezedwa mofulumira kwambiri – Kuchoka pokhala kapolo ndi kukhala nduna yayikulu ya Aigupto. M'nyengo iliyonse imene ife tingapezeke, tikuyenera kutenga kukhala nthawi yophunzira yomwe Mulungu wabweretsa pa miyoyo yathu.
2. Monga Farao anazindikira Yosefe kuti anali 'munthu amene mwa iye munali Mzimu wa Mulungu' ***(41: 38)***, choncho amene amakudziwani akuyenera kuona Mulungu mwa inu kudzera mu ntchito zanu zachifundo ndi moyo wanu wachiyero.

### MAWU OYAMBA
Yosefe anayitanidwa ku ndende ndipo anadzaonekera pamaso pa Farao. Luso lochokera kwa Mulungu lotanthauzira maloto lomwe Yosefe anali nalo linakondweretsa Farao, ndipo iye anamupatsa udindo waukulu wa 'Nduna yayikulu'. ***(Genesis 41: 41)*** Yosefe anali wokhulupirika pamaso pa Mulungu mu nthawi yake ya mavuto (Phunziro Loyamba) ndipo Mulungu analinso wokhulupirika kwa iye.

### KUTSIRIZA
**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Amatsenga ndi anthu anzeru analephera kumasulira maloto a Farao, koma Mulungu anawulula tanthauzo lake kwa Yosefe. ***(41: 8)***
2. Kupezeka kwa Mulungu m'moyo wa Yosefe ndiye zinamuthandiza kumasulira maloto n'chifukwa chake iye akupereka ulemu kwa Mulungu. ***(41: 16)***
3. Yosefe anafotokozera Farao ndondomeko yoti akhale ndi moyo zaka zisanu ndi ziwiri za njala ndipo anapulumutsa miyoyo yambiri mu Aigupto kuphatikiza ndi abale ake omwe amene ankakhala kutali kwambiri. ***(41: 33-36)***
4. Yosefe anakwezedwa ndipo anali wolamulira dziko la Aigupto. Iye anapatsidwa dzina latsopano ndiponso anapatsidwa mwana wa nduna yolemekezeka ya mu Aigupto kuti akhale mkazi wake, pofuna kuonetsa kuti anali wolemekezeka kwambiri. ***(41: 41-45)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**
**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Malo ake okwezedwa.

### KUKUMBUTSANA
Funsani ophunzira mafunso a za (i) maloto, (ii) kumasulira kwake, ndi (iii) kukwezedwa kwa Yosefe zomwe zidzawathandiza kuyankha mafunso molondola mu Phunziro Lachiwiri.

### KHALANI MOYO UMENEWU
**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Monga ngati Yosefe anali wokonzeka pa chilichonse chifukwa cha ubale wake ndi Mulungu, iye akuyenera kukhala chitsanzo chathu. Ngati ndife Akhristu, kupemphera ndi kuwerenga Baibulo ndi zofunika kwambiri kuti tidziwe chifuniro cha Mulungu ndi zochita pa miyoyo yathu.
2. Werengani Zowerenga Zoonjezera kuti mupeze zimene mlembi wa Masalimo, Davide, ndi Mtumwi Paulo ananena za Yosefe zaka zambiri iye atafa, ndipo gwiritsani zimenezi pa miyoyo yanu. ***Salimo 105: 16-22*** ndi ***Machitidwe 7: 9-10***
3. Yosefe anali wokonzeka kupereka ulemu kwa Mulungu ndipo ifenso tikuyenera kuchita zomwezo. Kudzipatsa tokha ulemu kumeneko ndiye kuba ulemu wa Mulungu.

| | **B7 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Moyo wa Yosefe**<br>**Mutu – Kukhululukira ndi nkhani yabwino!** | **B7 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Moyo wa Yosefe**<br>**Mutu – Mtima wake wosamalira** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 44: 18-34; 45: 1-14, 25-28***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 45: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngakhale abale ake a Yosefe ankafuna kumupha, Mulungu anagwiritsa ntchito maganizo awo oyipawo kuteteza miyoyo yawo, ndi kupulumutsa Aigupto ndi kukonzekera chiyambi ndi mtundu wa Israyeli.<br>2. Monga Yosefe anakanidwa kenaka anakhululukira abale ake, Mulungu amatikhululukira ndi kutidalitsa ngakhale tinamukana. | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 42 ndi 43***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aroma 14: 11-12***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Abale a Yosefe akuyenera kuthandizidwa kuti aone ndi kuvomereza tchimo lawo asanayanjanitsidwe.<br>2. Monga abale a Yosefe anagwada mogonja pamaso pake, moteronso aliyense adzayenera kugwada pamaso pa Ambuye Yesu Khristu tsiku limene adzabwera ndi kuvomereza kuti Iye ndi Ambuye. |
| **MAWU OYAMBA** | Pamene Yosefe anaona kuti abale ake anazindikira kulakwa kwawo, iye anawulula kuti anali ndani ndipo anati: ***"Ine ndine Yosefe." (Genesis 45: 4)*** Kambiranani ndi ophunzira kuti 'Yosefe wa kumwamba, Ambuye athu Yesu Khristu', nawonso anati Ine ndine pa mavesi awa: ***Yohane 6: 35 - mkate wamoyo; Yohane 8: 12 - kuunika kwa dziko lapansi; Yohane 10: 7 - khomo; Yohane 10: 11 - m'busa wabwino; Yohane 11: 25 - kuuka ndi moyo; Yohane 14: 6 - njira; Yohane 15: 1 - mpesa.*** | Nthawi yomaliza imene Yosefe anaona abale ake inali zaka makumi awiri zapitazo, pamene anamugulitsa kwa Amidyani, anthu ogula akapolo, pa mtengo wa ndalama zasiliva makumi awiri. Yosefe ankadabwa kuti mwina n'kutheka abale ake akadali oyipa mitima ndi osadalirika ngati nthawi imeneyo kapena kuti asintha patatha zaka zambiri. Iye anaganiza zowayesa m'njira zingapo kuti adziwe! |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kapu yasiliva inali chizindikiro cha ulamuliro wa Yosefe ndipo kuba kapu imeneyi unali mlandu woopsa kwambiri. Tsopano abale aja anali ndi nkhawa kuti Benjamini adzalangidwa kwambiri motero onse anabwerera ku nyumba yaufumu ya Yosefe, ndipo Yuda anadzipereka kuti alangidwe m'malo mwa Benjamini. ***(44:33)***<br>2. M'malo moti abale aja alangidwe analandira chikhululukiro ***(45: 5)*** ndipo Yosefe anafotokoza kuti Mulungu ankakwaniritsa cholinga chake pa moyo wake kudzera mu zimene iwo anamuchitira.<br>3. Abale aja anabwerera kwa Yakobo ndi nkhani yabwino yoti Yosefe ali moyo ndipo anaonetsa mphatso zomwe iye anatumiza kwa Yakobo. ***(45: 26-27)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhululukira ndi nkhani yabwino! | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Abale a Yosefe anabwera ku Aigupto kuti adzagule tirigu. Yosefe anawayankhula 'mwaukali' kuti iwo azindikire tchimo lawo asanakhululukidwe. ***(42: 6-7)***<br>2. Yosefe anawayika m'ndende masiku atatu. M'chikumbumtima chawo anazindikira kuti analakwira Yosefe ndipo anavomereza kulakwa kwawo ***(42: 21)***<br>3. Ngakhale Yosefe anawapatsa mwambo abale ake, iye anachita izi mwachikondi ndipo tikuona izi pa ***Genesis 42: 24*** pamene analira. Apa tikuona chisomo chenicheni chikugwira ntchito pamene Yosefe anapita kukaonetsa chokondi kwa abale ake amene sanali oyenera chikondi.<br>4. Pa ulendo wawo wachiwiri, kubwera ndi Benjamini kunali kuonetsa ulemu waukulu pamaso pake ndi kuvomereza ulamuliro wake. ***(43: 26-28)*** Pamenepa tikuona kukwaniritsidwa kwa maloto a Yosefe pa ***Genesis 37: 7***. Izi zikusonyeza kuti Mawu a Mulungu ndi owuziridwa ndi owona!<br>5. Yosefe anakhudzika mu mtima ataona Benjamini ndipo anapita mu chipinda china kukalira. ***(43: 30)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjera A – Mtima wake wosamalira. |
| **KUKUMBUTSANA** | Lumikizani phunziroli ndi Vesi Yoloweza: ***"Mulungu wandiyesa ine mwini Aigupto lonse"*** ndiye ***"Tsikirani kwa ine, musachedwe."*** Kambiranani ndi ophunzira za kusangalala kwa Yakobo pa ziganizo ziwirizi. ***(45: 9)*** | Phunzirani Mavesi Oloweza awiri ndi kukambirana ndi ophunzira momwe afotokozera phunziro lonse mwachidule. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kufunika kodziwa kuti Ambuye Yesu ali moyo Kumwamba ndipo ndi Ambuye wa onse, monga m'mene analili Yosefe ndi moyo ku Aigupto komanso wolamulira wa onse.<br>2. Kufunika kwa kumvetsetsa kuti Ambuye Yesu sadzatikhululukira kokha koma adzatipatsanso madalitso ochuluka tikadalira Iye.<br>3. Komanso, kumbutsani ophunzira kufunika koti ife titsatire chitsanzo cha Mulungu cha kukhululukira pokhululukira ena, monga mmene Ambuye Yesu anaphunzitsira m'pemphero lake kwa ophunzira. ***(Mateyu 6: 12)*** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi tikuphunzira chiyani za chisomo chomwe Ambuye Yesu amapereka pa ***Aroma 5: 21***?<br>2. Monga Yosefe anaonetsa chikondi kwa abale ake amene anamulakwira, ife tikuona Ambuye Yesu akuonetsa chikondi chachikulu pamene anafera ochimwa monga ife pa Kalvari. Werengani ***Luka 23: 34*** ndi kulingalira.<br>3. Maloto a Yosefe pa ***Genesis 37: 7-8*** anakwaniritsidwa pa ***Genesis 43: 26***. Werengani Zowerenga Zoonjezera, ***Salimo 51*** ndi ***Afilipi 2: 9-11*** ndi kulingalira ndime zimenezi ndi kutsindika kufunika kwa kuvomereza tchimo lathu ndi kufunika kovomereza 'Yesu Khristu Ambuye.' |

| | **B7 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Moyo wa Yosefe**<br>**Mutu – Onse pamodzi mu Aigupto** | **B7 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Moyo wa Yosefe**<br>**Mutu – Kukhululukira kwake kwathunthu** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 46: 1-7, 26-34***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Genesis 50: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kukhulupirika kwa Yosefe kunakhudza banja lake lonse ndi kubweretsa madalitso ambiri.<br>2. Yosefe ndi chitsanzo chenicheni cha lonjezo la Ambuye pa ***1 Samueli 2: 30*** limene likuti: ***"Amene andilemekeza Ine, Inenso ndidzawalemekeza iwowa."*** | **Ndime Yowerenga:** ***Genesis 44 ndi 45***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Aroma 5: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pamene abale a Yosefe anavomereza tchimo lawo ubale wawo ndi Yosefe unayambiranso, ndipo pamene tavomereza ndi kulapa tchimo lathu, timalowa mu ubale wabwino ndi watanthauzo ndi Ambuye Yesu.<br>2. Monga Yosefe anaperekera zinthu zochuluka kwa abale ake m'dziko la Aigupto, moteronso Ambuye Yesu adzapereka zochuluka kwa amene ndi ake ndi kuwatenga kupita nawo Kumwamba kumene akasangalala kwamuyaya. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozerani ophunzira momwe Mulungu akukwaniritsira cholinga chake pa moyo wa Yosefe. Banja lake lonse linachoka ku Kanani ndi kukhala ku Goseni, m'dziko la Aigupto. Dziko la Kanani linalonjezedwa kwa Abrahamu ndi zidzukulu zake koma Mulungu nthawi imeneyo ankachotsa banja la Yosefe pakati pa Akanani, anthu a makhalidwe oyipa amene anafulatira Mulungu. Koma, monga m'mene Mulungu analonjezera, mtundu wa Israyeli unadzabwerera ku dziko la Kanani. | M'phunziro lapita tinaphunzira momwe Yosefe anachitira mwaluso kuti athandize abale kuvomereza machimo awo. Njira yatsekuka tsopano yoti Yosefe awakhululukire ndi kuti ayanjanenso moona mtima ndi abale ake. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu akuwuza Yakobo kuti achoke kwawo ndi kupita ku dziko lachilendo kutali ndipo akumutsimikizira adzamusamalira. ***(46: 2-3)***<br>2. Banja lonse pamodzi ndi katundu wawo akupita ku Aigupto. ***(46: 5-7)***<br>3. Banja la Yakobo likufika ku Goseni ndipo mwa misozi ya chimwemwe ikutsika pakati pa Yosefe ndi Yakobo. ***(46: 29)***<br>4. Yakobo atamwalira, abale aja anaopa kuti mwina Yosefe adzawabwezera zomwe anamuchitira, koma, modabwitsa aliyense, iye sanangowakhululukira kokha koma analonjeza kuwasamalira pamodzi ndi mabanja awo. ***(50: 15-21)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Onse pamodzi mu Aigupto. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Abale ake asanachoke kubwerera kwa abambo awo Yakobo, Yuda anadzipereka kutsala ku Aigupto kuti agwire ntchito monga kapolo m'malo mwa Benjamini. Uku kunali kusinthika kwakukulu kuchokera pa nthawi anagulitsa Yosefe ku ukapolo ndi kubweretsa madandaulo pa moyo wa Yakobo kwa zaka zambiri! Tsopano chisomo cha Mulungu chinkagwira ntchito m'mitima mwawo. ***(44: 33)***<br>2. Yosefe akudziwulula kwa abale ake ndi kuwawuza kuti Mulungu analepheretsa zoyipa ndi kuchita zabwino. ***(45: 4-5)***<br>3. Yosefe akulira, akukhumbatira Benjamini ndi kupsopsona abale ake onse. ***(45: 14)***<br>4. Farao akuwuza Yosefe kuti awuze abale ake kuti abweretse abambo ake ndi mabanja awo ku Aigupto kuti adzawasamalire. ***(45:17-19)***<br>5. Abale akuwuza Yakobo kuti Yosefe ali moyo ndipo pamene anaona ngolo zomwe iye anatumiza kuti akwere popita ku Aigupto, Yakobo anadziwa kuti Yosefe ali moyo ndipo adzakumananso naye! ***(45: 25-28)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhululukira kwake kwathunthu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Funsani ophunzira mosamala kuti mafunsowo awathandize kulemba mayankho a mafunso a mu phunziro lachinayi. | Thandizani ophunzira kuti azindikire kuti 'Nkhani Yabwino' ya Yosefe ndi yofanana ndi 'Nkhani Yabwino' ya Ambuye Yesu:<br>1. Monga momwe Yosefe anali moyo, Yesu ndi wamoyo lero.<br>2. Monga momwe Yosefe anali wolamulira mu Aigupto, nawo Ambuye Yesu ndi Mfumu ya Mafumu ndi Ambuye wa Ambuye<br>3. Monga momwe Yosefe anasamalira banja lake, Ambuye Yesu anapereka chilichonse chimene tikuchifuna kuti tipulumutsidwe.<br>4. Monga momwe Yosefe anabweretsa banja lake ku Aigupto, Ambuye Yesu akufuna ife tibwere kwa Iye kuti tipulumutsidwe ndi kuti tikakhale Kumwamba kwamuyaya. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga ngati Yosefe amene mwina ankadabwa nthawi zambiri za tsogolo lake, ifenso nthawi zonse sitidziwa zomwe zidzatichitikira. Koma monga Akhristu titha kukhala ndi chitsimikizo kuti Mulungu adzalemekeza kukhulupirika kwathu.<br>2. Mulungu amalepheretsa zolinga zoyipa za maboma a dziko lapansi lero ndipo amakwaniritsa zolinga zake pa zimene akufuna zichitike. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ife tikuyenera kufuna kuvomereza ndi kulapa tchimo lathu, ndi kukhulupirira Ambuye Yesu amene anatifera. Kenaka tidzadziwa chikhululukiro ndipo tidzakhala okonzeka kukhululukira ena.<br>2. Mulungu anali ndi Yosefe ndipo izi zinayankhulidwanso ndi Stefano asanaphedwe m'Chipangano Chatsopano patapita zaka zambiri, monga alemba mu Zowerenga Zoonjezera. ***(Machitidwe 7:12-15)*** |

| | **B8 – KALASI 3**<br>**Phunziro Loyamba – Alembi a Uthenga Wabwino**<br>**Mutu – Mateyu** | **B8 – KALASI 4**<br>**Phunziro Loyamba – Zoyenera Kuchita**<br>**Mutu – Akhristu kusonkhana pamodzi** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 9: 9-13 ndi 27: 37-42***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 16: 16***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pamene Yesu anayitana Mateyu, Myuda, wolandira misonkho, iye anavomera nthawi yomweyo ndi kuyamba kutsatira Yesu.<br>2. Koma Ayuda ambiri anakana kulandira Yesu ndipo, zotsatira zake, Iye anapachikidwa. | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 2: 41-44; 4: 32-35***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 2: 42***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pamene anthu akhala Akhristu, amazindikira kufunika kosonkhana pamodzi pakati pawo ndi cholinga choti akule mu chikhulupiriro chawo.<br>2. Iwo amafunanso kumathandizana pa chilichonse chimene angathe kuchita komanso kugawa zomwe ali nazo. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozerani ophunzira kuti Mateyu ankagwira ntchito yolandira misonkho. Ayuda ankawadana anthu amenewa chifukwa cha chinyengo chawo, kukweza misonkho imene ankalandira kwa anthu ndiponso chifukwa ankatumikira zolinga za Ufumu wa Chiroma umene unkazunza Ayuda nthawi imeneyo. | Fotokozerani ana kuti Petro anali m'modzi mwa ophunzira a Yesu ndipo anakana Yesu pamene ankapachikidwa. Koma Yesu anamukhululukira ndipo tsopano akuwuza anthu za Yesu molimba mtima. Zolakwa zake sizinali zoti sangakhululukidwe nazo ndipo tsopano Mulungu akumugwiritsa ntchito mwa mphamvu. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mateyu anavomera nthawi yomweyo kuyitana kwa Mpulumutsi.<br>2. Mateyu anasiya ntchito yake yachinyengo ija nthawi yomweyo ndi kukhala wophunzira wa Ambuye Yesu. Iye anali m'modzi wa ophunzira khumi ndi awiri aja. ***(9: 9)***<br>3. Iye anapatsidwa ulemu wolemba Uthenga Wabwino wa Mateyu ndi kuonetsa kuti Yesu ndi Mfumu imene akhala akuyembekezera nthawi yayitali yomwe Ayuda ankati ndi Mesiya.<br>4. Mwachidule fotokozani zomwe Mateyu akufotokoza za kubwera kwa Ambuye Yesu ndiponso tsindikani kuti Mateyu ndiye akufotokoza ndime zambiri za m'Chipangano Chakale zonena za Ambuye Yesu kuonetsa kukwaniritsidwa kwake pamene anabwera pa dziko lapansi. ***(Mateyu 1 ndi 2)***<br>5. Mateyu akulemba m'bado wa Yesu, utumiki wake kwa anthu ndipo akutsiriza ndi kuzengedwa mlandu, kuyikidwa m'manda ndi kuuka kwake – maziko a chipulumutso chathu zotsatira zake buku lake likutchedwa 'Uthenga Wabwino'. Onani mayina awiri pa pepalapo. "Mfumu imene inalonjezedwa kale", ndi "Mfumu imene inakanidwa ndi kupachikidwa".<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A - Mateyu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Petro, m'modzi mwa ophunzira a Yesu, analalikira Uthenga Wabwino kwa anthu ambiri ndi kuwafotokozera kufunika kwa kulapa machimo awo ndi kuyamba kukhulupirira Khristu wamoyo. Anthu ambiri anakhala Akhristu ndi kukhulupirira Yesu Khristu monga Mpulumutsi – anthu 3,000 anaonjezeka pa anthu 120 amene anali kale mu Mpingo! *Kambiranani ndi ophunzira za kupambana kwa tsiku limeneli poona anthu ochuluka akukhala Akhristu mofulumira.* ***(2: 38-41)***<br>2. Akhristu atsopanowa anayamba kuchitira zinthu pamodzi m'dera lawo – uku kunali kuyamba kwa mpingo. Iwo anali amodzi ndi Akhristu ena, pamene ankamvera ziphunzitso za atumwi, ndipo ankakhala nawo pa chiyanjano ndi pa mwambo okumbukira imfa ya Ambuye Yesu ndi m'mapemphero. Fotokozerani ophunzira kuti akuyenera kumasonkhana anthu amene adzawathandiza kuphunzira Mawu a Mulungu, kupemphera ndi kukula mu chikhulupiriro. ***(Machitidwe 2: 42)***<br>3. Akhristu anakumana pamodzi ndi kumagawana zinthu zawo. Izi sizikutanthauza kuti ankagawana ndi wina aliyense koma okhawo amene anali ndi zosowa, monga banja. Iwo anazindikira kufunika kokhala monga abale ndi alongo mwa Khristu ndiponso za tanthauzo la kugawana wina ndi mnzake ndiponso kukondana mwa Khristu. ***(Machitidwe 2: 42-47)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Akhristu kusonkhana pamodzi. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziroli pofunsa ophunzira mafunso amene awathandize kuyankha mafunso a Phunziro Loyamba. | M'magulu a awiriawiri, lembani zomwe Akhristu angachite kuti akule ndi kukhwima mu chikhulupiriro lero monga gulu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. N'kofunika kuyankha ndi kupereka msanga miyoyo yathu kwa Ambuye Yesu.<br>2. Dziwani kuti Yesu sanali Mfumu ya Ayuda yokha komanso Mfumu ya Mafumu ndi Ambuye wa Ambuye, motero ndi woyenera kumudalira ndi kumutumikira.<br>3. Zindikirani kuti Ambuye Yesu sankayenera kudzipulumutsa yekha ndipo kuti kunali kofunika kuti Iye akhale pa mtanda kuti apulumutse ochimwa monga ife. Yankhulani izi kwa ophunzira: *'Iye yekha sakanadzipulumutsa, Iye pa mtanda anayenera kufa, kupanda kutero chifundo sichikanabwera pafupi ndi ochimwa; Inde, Khristu Mwana wa Mulungu anakhetsa magazi kuti ochimwa amasulidwe.'* – Albert Midlane | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ngati ndife Akhristu, kodi timakhala ndi nthawi yosonkhana ndi Akhristu anzathu, mu chiyanjano ndi kuphunzira kuchokera kwa wina ndi mnzake? Ife sitingakule m'moyo wauzimu popanda kuwerenga Mawu a Mulungu ndi kupemphera pamodzi.<br>2. Tikuyenera kuganiza za udindo wathu othandizana wina ndi mnzake njira iliyonse tingathe, monga abale ndi alongo mwa Khristu. Banja la Mulungu limagwira bwino ntchito pamene akugwirira limodzi.<br>3. Kodi mukuganiza mwachita zolakwa zambiri ndipo simungathe kutumikira Yesu? Petro anakana Yesu, koma anagwiritsidwa ntchito kuti alalikire kwa gulu lalikulu kwambiri Uthenga Wabwino – Mulungu atha kuchitanso zomwezo ndi moyo wanu! |

| | B8 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Alembi a Uthenga Wabwino<br>Mutu – Marko | B8 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Zoyenera Kuchita<br>Mutu – Ubatizo wa Chikhristu |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Machitidwe 12: 5-12, Marko 1: 29-42***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 10: 45***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Marko mu Uthenga wake Wabwino wakhazikika pa Yesu ngati 'Mtumiki wangwiro' ndipo akulemba zambiri zomwe anachita kuposa zomwe anayankhula.<br>2. Marko akuonetsa momwe Ambuye Yesu akusankhira ena oti atumukire. | **Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 28: 16-20, Machitidwe 8: 34-39 ndi 18: 8***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 2: 41***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ubatizo ndi chizindikiro cha kumvera Khristu.<br>2. Anthu ambiri m'Baibulo amene anakhala Akhristu anabatizidwa ngati chizindikiro cha chikhulupiriro chawo.<br>3. Ubatizo ndi chionetsero pa gulu kuti ukutsatira Khristu. |
| **MAWU OYAMBA** | Mu Uthenga Wabwino wa Marko muli nkhani ya Ambuye Yesu amene anachokera Kumwamba ndi kubwera pa dziko lapansi osati kudzatumikiridwa koma kudzatumikira ndi kupereka moyo wake pa mtanda wa Kalvari (monga Vesi Yoloweza). Pamene anali pa dziko lapansi, Ambuye Yesu anamvera mokhulupirika chifuniro cha Mulungu ndipo ntchito yake ya mphamvu inachitika mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. Ndi zokondweretsa kuti Marko, mlembi, anayamba bwino, kenaka anapuma pang'ono ntchito, ndipo potsiriza anagwira ntchito modzipereka kwambiri ***(2 Timoteo 4: 11)*** ya Ambuye. | Funsani ana ngati anapita kumene ankabatiza anthu kapena ngati iwo anabatizidwa. Afunseni kuti afotokoze zomwe iwo akudziwa, kuti zinali zotani. Chinachitika ndi chiyani? Kodi ankaganiza kuti unkayimira chiyani? |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Marko ankachokera ku banja limene nyumba yawo Akhristu a mu Yerusalemu anagwiritsa ntchito kupempherera Petro kuti apulumutsidwe kwa Herode, imene anapha Yakobo. ***(Machitidwe 12: 5-12)***<br>2. Marko anafuna kutumikira Mulungu pofalitsa Uthenga Wabwino koma ngakhale anapita ndi Paulo ndi gulu lake ulendo woyamba, iye anawasiya ndi kubwerera ku Yerusalemu. ***(Machitidwe 12: 25, ndi 13: 13)***<br>3. Paulo anaona ngati kufooka kwa Marko pamene anathawa ku utumiki ndipo sanalole kuti apite naye pa ulendo wachiwiri. ***(Machitidwe 15: 37-39)*** Koma, patapita nthawi Marko anabwezeretsedwa ndipo Paulo anayamba kumukhulupirira, ndipo anapitiriza kutumikira Ambuye Yesu.<br>4. Ngakhale Marko analephera mu utumiki, ndi iye analemba Uthenga Wabwino wa Marko onena zambiri zomwe Ambuye Yesu anachita pamene anali pa dziko lapansi, makamaka zodabwitsa zake. Iye anaonjezera za nkhani ya kuchiritsidwa kwa mpongozi wa Simoni, kuyeretsedwa kwa wakhate ndi kuletsa namondwe pamene ophunzira anali m'bwato pa Nyanja ya Galileya.<br>5. Tsindikani mitu awiri pa pepalapo: "Marko akufotokoza kuti Yesu ndi Mtumiki Wangwiro", "Marko akuonetsa kuti Ambuye Yesu amagwiritsa ntchito ena kuti amutumikire".<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Marko. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu asanachoke pa dziko lapansi, anapereka Lamulo Lalikulu kwa ophunzira ake. Apa ndi pamene anawawuza kuti apite ku dziko lonse lapansi ndi kukapanga ophunzira ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Yesu analonjeza kukhala nawo pamene akuchita zimenezi. Iye anawapatsa ulamuliro ochitira zimenezi. ***(Mateyu 28: 18-20)***<br>2. Yesu anawuza ophunzira ake kuti azibatiza anthu. Ubatizo umayanjanitsa okhulupirira ndi Yesu Khristu mu imfa yawo ku tchimo ndi kuuka kwawo kwa akufa kuti akhale moyo watsopano. Iwo ali ndi moyo watsopano pamene akhale Akhristu. Iwo amasiya moyo wawo wakale, ndi kuyamba mwatsopano, chifukwa cha magazi a Yesu amene anakhetsa pa mtanda. Ubatizo ndiye chizindikiro cha zimenezi pamaso pa aliyense. ***(Aroma 6: 3-7)***<br>3. Ubatizo umayimira kugonjera Khristu, kukonzeka kukhala moyo monga m'mene Mulungu afunira, ndipo kuyanjana ndi anthu amene ali pa pangano ndi Mulungu.<br>4. Pa nkhani ya pa ***Machitidwe 8***, Filipi akuwuza nduna ya ku Aitiopiya Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Iye anakhala Mkhristu ndipo nthawi yomweyo anabatizidwa.<br>5. Pa ***Machitidwe 18: 8***, Paulo, mtumwi, akubweretsa anthu ambiri kwa Yesu Khristu. Ubatizo ukuchitika nthawi yomweyo atakhulupirira.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Ubatizo wa Chikhristu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziroli pogwiritsa ntchito mafunso awa:<br>1. Kodi Marko akuonetsa motani Ambuye Yesu mu Uthenga wake Wabwino wonse?<br>2. Kodi Marko anachokera banja lotani? Chifukwa chiyani?<br>3. Kodi Marko ankafuna kuchita chiyani ndi moyo wake?<br>4. Ngakhale Marko anakhumudwitsa Paulo pa ulendo wake woyamba wokalalikira, kodi tikudziwa bwanji kuti anabwezeretsedwa kwathunthu mu utumiki?<br>5. Tchulani zina zomwe Yesu ankachita ali pa dziko lapansi. | Phunzirani Lamulo Lalikulu. ***(Mateyu 28: 16-20)***<br>1. Kodi Yesu akhoza kulamulira zimenezi motani? ***(vesi 18)***<br>2. Kodi ndi malangizo anayi ati amene anawapatsa ophunzira aja?<br>3. Kodi kukhala wophunzira zimatanthauza chiyani? Kodi ndi zochitika nthawi zonse?<br>4. Kodi Yesu akulonjeza chiyani iwo akatsatira zomwe walamula? |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Tchulani ntchito imene mungagwire potumikira Ambuye Yesu.<br>2. Tikhoza kupita m'tsogolo mu utumiki ngakhale tinalepherapo m'mbuyomo.<br>3. Tikhoza kudalira Yesu pa nthawi ya mayesero ndi namondwe wa moyo wathu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi munapereka moyo wanu kwa Yesu ndipo mukufuna kukhala moyo wokondweretsa iye m'moyo wanu watsopano?<br>2. Kodi munabatizidwa pomvera Mawu ake? Ngati ayi, ndi chifukwa chiyani? |

| | **B8 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Alembi a Uthenga Wabwino**<br>**Mutu – Luka** | **B8 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Zoyenera Kuchita**<br>**Mutu – Mgonero wa Ambuye** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 1: 1-4; 4: 1-13***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 19: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Luka akutsindika kuti pokhala Iye Mwana wa Mulungu, Ambuye Yesu anali munthu 'Wangwiro'.<br>2. Mayesero anasonyeza kuti Ambuye Yesu sanachimwe ndipo, pakuti anali woyera, munthu wopanda tchimo, Iye ndiye akanatha kukhala Mpulumutsi wa anthu ochimwa. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 22:14-20, 1 Akorinto 11: 23-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Akorinto 11: 26***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu analamula kuti tizimukumbukira mwapadera.<br>2. Ife tikuyenera kutenga chikumbutso ichi kukhala chapadera kwambiri. |
| **MAWU OYAMBA** | Ngakhale Luka ndi Machitidwe analembera Teofilo, ife tikudziwa zochepa za iye. Mawu akuti, 'wolemekezeka' ***(Luka 1:3)*** akutionetsa kuti anali mkulu wa boma. Dzina lake likutanthauza kuti 'bwenzi la Mulungu'. Mwina iye anali Mkhristu wa udindo m'boma la Aroma. Luka anamulembera zonse zokhudzana ndi moyo wa Yesu pofuna kutsutsa zabodza zomwe anthu ankayankhula. | Funsani ophunzira kuti aganizire zomwe angachite pofuna kukumbukira wina amene anawasiya, pogwiritsa ntchito zithunzi kapena tsiku lapadera. Yesu anawasiyira ophunzira ake njira yapadera yoti azimukumbukira pamene adzakhala atachoka pakati pawo. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Luka anali munthu wa Amitundu, dokotala wa Chikhristu amene anali mnzake wa mtumwi Paulo. ***(Akolose 4: 14)***<br>2. Luka akufotokoza za Yesu pa kubadwa kwake kuti ndi 'Mpulumutsi, amene ali Khristu Ambuye'. ***(Luka 2: 11)*** Iye anali Mulungu m'thupi la munthu.<br>3. Luka akulemba kuti Iye anali wangwiro kwathunthu pamene ankakula. ***(Luka 2: 52)*** Kukula mu nzeru kwa Ambuye zikuonetsa kuti anakula m'chidziwitso chake, Kukula mu msinkhu zikusonyeza kukula kwa thupi lake; kukula pa 'chisomo ndi Mulungu' zikusonyeza kukula pa moyo wake wauzimu; ndipo kukula pa 'chisomo ndi anthu' zikusonyeza kukhala pa ubale wabwino ndi anthu ena.<br>4. Fotokozani mwachidule za mayesero a Yesu ***(Luka 4:1-13)*** ndipo onetsani kuti zimenezi zikusonyezanso kuti Iye anali munthu wangwiro amene sanagonjere mayesero.<br>5. Pa Luka 23, tili ndi nkhani ya kufa kwa Ambuye ndi ndemanga zabwino zomwe anapereka Pilato, m'modzi wa anthu achifwamba, ndi kenturiyo, zomwe zinaonetsanso ungwiro wa Ambuye Yesu. ***(Luka 23: 14, 41 ndi 47)*** *Fotokozani kuti ndi zofunika kuti Yesu akhale wopanda tchimo; ngati si choncho Iye sakanatha kufera machimo athu. Lero Munthu Wangwiro ameneyu ali Kumwamba ndipo akufuna kupulumutsa ochimwa. Iye akusamaliranso amene ndi ake ndipo anamukhulupirira kukhala Mpulumutsi ndi Ambuye wawo.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Luka. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Usiku womaliza umene ophunzira ndi Yesu anali pamodzi, Yesu anatenga mkate ndi vinyo ndipo anayamika. Iye anati mkate ndi thupi lake limene likuperekedwa chifukwa cha iwo, ndipo vinyo anali magazi ake amene akukhetsedwa chifukwa cha iwo. Kenaka anawawuza kuti adye mkate ndi kumwa vinyo ngati chikumbutso chake. ***(Marko 14: 22-25)***<br>2. Ophunzira sankamvetsetsa pakuti ndi Yesu yekha amene ankadziwa zomwe ziti zichitike. Koma ophunzira ankayenera kukumbukira lamulo lake.<br>3. Iyi ndi njira yapadera kwa Akhristu yoti aziganizira ndi kulingalira za imfa ndi masautso a Ambuye Yesu, pamene akudya mkate ndi kumwa vinyo. ***(1 Akorinto 11: 23-26)***<br>4. Monga Paskha chinali chikondwerero cha kuomboledwe kwa Israyeli mu ukapolo m'dziko la Aigupto, motero podya mkate ndi kumwa vinyo ndi chikondwerero cha kumasulidwa kwathu ku tchimo kudzera mwa Khristu.<br>5. Ambuye Yesu anawuza ophunzira ake kuti azidya mkate ndi kumwa vinyo mpaka Iye adzabwerenso. Ichi sichinali chikumbutso chokha cha moyo ndi imfa ya Yesu komanso chinali chikumbutso cha ufumu wa Mulungu!<br>6. Iye anafuna kudya Paskha ameneyu ndi ophunzira ake pamene Yesu mwini ankayenera kukhala Mwanawankhosa wa Paskha, woperekedwa chifukwa cha machimo a anthu. Uwu unali mwambo oyimirira thupi ndi magazi ake kwa ophunzira. ***(1 Akorinto 5: 7)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Mgonero wa Ambuye. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziroli pofunsa mafunso awa:<br>1. Kodi mutu wa Uthenga Wabwino wa Luka ndi wotani?<br>2. Kodi Luka ankagwira ntchito yanji?<br>3. N'chifukwa chiyani analembera Teofilo?<br>4. Kodi kufunika kwa mayina amene Yesu anapatsidwa akubadwa akuti 'Mpulumutsi, amene ali Khristu Ambuye' n'kotani?<br>5. N'chifukwa chiyani Luka akulemba za mayesero?<br>6. Onani pa ***Luka 23: 14, 41 ndi 47*** ndi kukambirana zomwe anthu awa ananena za 'Munthu Wangwiro'. | Pa ***1 Akorinto 11: 27-31***, akuti tikuyenera kudziyesa tokha tisanadye chakudya cha chikumbutso chake. Kambiranani zomwe mukuganiza kuti ndi tanthauzo lake. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi mumaona motani Ambuye Yesu – monga 'Munthu Wangwiro' kapena munthu ngati wina aliyense?<br>2. Kodi inu munakhulupirira Munthu Wangwiroyu kukhala Mpulumutsi wanu? Ngati munatero, kodi mukuwuza ena za Iye? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ife monga Akhristu timatenga mkate ndi vinyo motsimikiza zomwe zikuyimira?<br>2. Kodi timayamika kuti "mu pangano latsopano" sitipereka nsembe kudzera mwa ansembe koma tokha tifika pamaso pa Mulungu chifukwa cha Yesu? |

| | B8 – KALASI 3<br>Phunziro Lachinayi – Alembi a Uthenga Wabwino<br>Mutu – Yohane | B8 – KALASI 4<br>Phunziro Lachinayi – Zoyenera Kuchita<br>Mutu – Kukula kwa Mkhristu |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yohane 20: 26-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 20: 31***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yohane akutsindika kuti Yesu ndi 'Mwana wa Mulungu'.<br>2. Yesu anagwiritsa ntchito mawu akuti 'Ine ndine' nthawi zambiri ndipo potero ankanena kuti Iye anali wofanana ndi Mulungu pakuti Mulungu anadzitcha yekha kuti 'Ine ndine' m'Chipangano Chakale. ***(Eksodo 3: 14-15)*** | **Ndime Yowerenga:** ***1 Petro 2: 1-3, 2 Petro 3: 18, Machitidwe 17: 10-12***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Petro 2: 2***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Akhristu akuyenera kukula tsiku ndi tsiku pa chikhulupiriro chawo.<br>2. Pali zambiri zoti tiphunzire za chisomo ndi chidziwitso cha Mulungu pa aliyense. |
| **MAWU OYAMBA** | Yohane akuyamba Uthenga Wabwino ponena kuti Yesu ndi 'Mawu'. ***(Yohane 1: 1)*** Mawu ndi amene timagwiritsa ntchito pofotokoza kapena polumikizana ndi ena. Mulungu anadzifotokoza yekha m'dziko lapansi kudzera mwa Mwana wake, Ambuye Yesu Khristu, pamene Mwana wa Mulungu anakhala Mwana wa Munthu, wobadwa mwa namwali, Mariya wa ku Betelehemu zaka zoposa 2000 zapitazo. Pofera ife, Iye anaonetsa momwe Mulungu amatikondera ndipo motero Iye ndiye maganizo enieni a Mulungu pa ife. | Kambiranani ngati gulu m'mene zinthu zimakulira monga, nyama, ana, zodzala ndi mitengo. Kodi pamafunika chiyani kuti zikule? Kodi chimachitika ndi chiyani ngati sizikulandira zinthu zofunika? |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yohane akuti Yesu ndi 'Mawu'. ***(Yohane 1: 1)***<br>2. Yohane akuti iye ndi 'wophunzira amene Yesu ankamukonda'. (***Yohane 20: 2***)<br>3. Mu Uthenga Wabwino wa Yohane, 'Ine ndine' ndi dzina la Mulungu, ndipo Yesu anafotokoza za khalidwe la Mulungu m'njira zisanu ndi ziwiri:<br>Mkate Wamoyo. ***(Yohane 6: 35, 41, 48, 51)***<br>Kuunika kwa dziko lapansi. ***(Yohane 8: 12; 9: 5)***<br>Khomo. ***(Yohane 10: 7, 9)***<br>M'busa Wabwino. ***(Yohane 10: 11, 14)***<br>Kuuka ndi Moyo. ***(Yohane 11: 25-26)***<br>Njira, Choonadi ndi Moyo. ***(Yohane 14: 6)***<br>Mpesa. ***(Yohane 15: 1, 5)***<br>4. Yohane analemba Uthenga Wabwino kuti ife tikhulupirire Ambuye Yesu ndi kukhala ndi moyo wosatha. ***(Yohane 20: 30-31)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yohane. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Monga Mkhristu, pali momwe tikuyenera kukhalira. Ife timayenera kuonetsa Khristu pa makhalidwe ndi zochita zathu. M'Baibulo muli mavesi ambiri amene angatithandize kudziwa momwe tikuyenera kukhalira moyo wolemekeza Mulungu.<br>2. Pa ***1 Petro 2: 1***, akutiwuza kuti tisakhale achinyengo, achiphamaso ndi ansanje kapena oyankhula zopanda pake.<br>3. ***1 Petro 2: 2*** - akunena kuti Mkhristu watsopano ali ngati mwana wakhanda. Kuti akule, iwo akuyenera kumamwa mkaka. Mkaka umenewu ndi Mawu a Mulungu. Kukula kumeneku sikumasiya ndipo monga mwana akamakula, amayenera kumadya. M'njira yomweyonso, palibe nthawi m'moyo wa Mkhristu pamene safunanso chakudya (Baibulo) kuti chimuthandize kukula.<br>4. ***2 Petro 3: 18*** akutiphunzitsa kukula mu chisomo ndi mu chidziwitso cha Ambuye athu. *Kambiranani ndi ophunzira kuti chisomo ndi chidziwitso ndi chiyani ndiponso momwe tingakulire.*<br>5. Pamene Paulo ndi Sila ankalalikira Uthenga Wabwino ku Bereya, anthu anali okondweretsedwa ndi osangalala ndi zomwe iwo ankayankhula. Pa ***Machitidwe 17***, akuti iwo anali omasuka kwambiri ndipo ankamvera mwachidwi ndi kumafufuza m'Malemba tsiku ndi tsiku. Ichi chinali chidwi chachikulu pophunzira za Mulungu!<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukula kwa Mkhristu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Tengani chimodzichimodzi cha chomwe Iye ali pa zinthu zisanu ndi ziwiri zomwe Iye wanena kuti 'Ine ndine' ndipo mukambirane momwe chilichonse chikuonetsera kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. | Anthu a ku Bereya amene Paulo ndi Sila anawayankhula ***(Machitidwe 17: 10-12)*** anali ndi chidwi chophunzira ndi kufufuza Malemba kuti aone ngati zomwe Paulo ndi Sila akunena zinali zoona.<br>Ife tikuyenera kusamala osamangoti chilichonse chimene mlaliki kapena mtsogoleri akuyankhula kuti ndi zoona. Ife tikuyenera kumafufuza tokha mayankho kuchokera m'Baibulo. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Funsani ophunzira kuti anene ngati akukhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu.<br>2. Ngati akutero, kodi anakhulupirira Iye ndi kulandira moyo wosatha? ***(Yohane 1: 12-13; 5: 24)***<br>3. Ngati ife talandira moyo wosatha, ndiye kuti tikupita Kumwamba ndipo tikuyenera kumawerenga Baibulo tsiku ndi tsiku kuti tidziwe chifuniro cha Mulungu pa miyoyo yathu. Komanso tikuyenera kumapemphera tsiku ndi tsiku ndi kumayamika Ambuye Yesu chifukwa cha chifundo chake pa ife ndiponso kumupempha kuti atipatse mphamvu zoti zitithandize kuchita zomwe Baibulo likunena kwa ife. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi timafuna kukula tsiku ndi tsiku? Kodi timawerenga ndi kupemphera ndi cholinga chofuna kuphunzira zambiri za Mulungu kuti chikhulupiriro chathu chikule? Tikaphunzira Mawu a Mulungu motsogozedwa ndi Mzimu Woyera ndi pamene tidzakula.<br>2. Kodi ife tikufanana ndi anthu a ku Bereya motani? Kodi timamvetsetsa pamene akutiphunzitsa? Kodi timasanthula Malemba tsiku ndi tsiku kuti tipeze mayankho?<br>3. Kambiranani momwe tingatsimikizire kuti Baibulo ndi Mawu a Mulungu. |

| | **B9 – KALASI 3**<br>**Phunziro Loyamba – Mose**<br>**Mutu – Mwana mu dengu** | **B9 – KALASI 4**<br>**Phunziro Loyamba – Mose**<br>**Mutu – Kalonga** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 1: 6-20 ndi 22; 2: 1-10***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11: 23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Aisrayeli anachulukana ndipo anali ndi mphamvu zambiri mu Aigupto, motero Farao anaganiza kuti anthuwa atha kudzakhala mbali ya adani ake nthawi ya nkhondo, choncho analamula kuti ana aamuna onse aziwapha akangobadwa.<br>2. Mulungu anali ndi chikonzero chodzagwiritsa ntchito Mose kugonjetsa Farao ndi kumasula Aisrayeli mu ukapolo, choncho anateteza Mose pamene anali khanda kuti asamire mu Mtsinje wa Nailo. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 1: 5-22; 2: 1-25***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11: 23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Aisrayeli anachulukana ndipo anali ndi mphamvu zambiri mu Aigupto, motero Farao ankaganiza kuti iwo anali chiopsezo kwa iye pa nthawi ya nkhondo, choncho analamula kuti ana onse aamuna akangobadwa aziphedwa.<br>2. Mulungu anali ndi cholinga ndi moyo wa Mose – iye ankayenera kupulumutsa ana a Israyeli m'dziko la Aigupto. |
| **MAWU OYAMBA** | Bwerezani maphunziro a B6 ndi B7 ndipo fotokozani kwa ophunzira kuti patapita zaka 300 Yosefe ndi abale ake atafika mu Aigupto; Aisrayeli anachulukana kwambiri. Farao watsopano anakhala pa mpando amene anawasandutsa akapolo. Nthawi yomweyi, Mulungu ankakonza njira yoti apulumukire kudzera mu kubadwa ndi kutetezedwa kwa Mose. Ndi Mose amene adzawatsogolera kupita ku Kanani. | Bwerezani Maphunziro B6 ndi B7. Fotokozani kuti Yosefe ankamwalira, ana a Israyeli anali banja limodzi lalikulu kwambiri. Koma kenaka anasanduka mtundu waukulu, zomwe zinachititsa mantha Farao watsopano amene anawasandutsa akapolo.<br>Koma Mulungu sanawayiwale ndipo anachita zotheka kuti cholinga chake chikwaniritsidwe pa mtundu wa Israyeli. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Farao anayamba kulamulira ndipo kulemera kwa Aisrayeli ***(1: 7)*** kunawabweretsa masautso ***(1: 8-11)***, koma Mulungu ankayang'anira ndi kuwateteza. ***(1: 12)***<br>2. Farao analamula kuti ana onse aamuna akhanda aziphedwa pobadwa ndi cholinga chofuna kuchepetsa chiwerengero chawo. ***(1: 15-20)***<br>3. Mose anali mwana wa Amramu ndi Yokobedi ndipo atamusunga m'nyumba miyezi itatu, iwo anamuyika m'dengu lomwe anakalisiya m'mbali mwa Mtsinje wa Nailo. ***(2: 1-3)***<br>4. Mulungu anateteza moyo wa Mose pogwiritsa ntchito Miriamu, mlongo wake, amayi ake ndi mwana wamkazi wa Farao. ***(2: 4-9)***<br>5. Mose analandira maphunziro apamwamba kwambiri chifukwa anali 'mwana wa mwana wamkazi wa Farao' ***(Machitidwe 7: 22)*** ndipo anali wolowam'malo mu ufumu wa ku Aigupto.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mwana mu dengu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Farao ankachita mantha poganiza kuti Aisrayeli adzakhala chiopsezo mu ufumu wake, choncho anawasandutsa akapolo ndi cholinga choti asachulukanenso. ***(1: 8-11)***<br>2. Aisrayeli anayamba kukhala amphamvu kwambiri, choncho Farao analamula anamwino kuti azipha mwana wamwamuna aliyense akungobadwa, koma anamwino sanamvere lamulo lake ndipo anapulumutsa miyoyo ya anawo. ***(1: 15-20)***<br>3. Pamene Mose ankabadwa, anapanga kabwato kakang'ono ndipo amayi ake anamuyika m'menemo m'mbali mwa Mtsinje wa Nailo. ***(2: 1-3)***<br>4. Mwana wamkazi wa Farao ndiye anapulumutsa Mose ndipo kenaka amayi ake ndiye amene anamusamalira. ***(2: 4-9)***<br>5. Mose anakulira m'nyumba yaufumu. Iye atakula, anayamba kudzionetsa kuti anali ndi mphamvu zothandiza akapolo a Chisrayeli.<br>6. Iye akupha Maigupto amene ankamenya kapolo ndipo kenaka anathawa kupita ku dziko la Midyani. ***(2: 11-15)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kalonga. |
| **KUKUMBUTSANA** | Funsani ophunzira kuti afotokoze mwachidule m'ziganizo zochepa, zomwe iwo aphunzira:<br>(i) Mbiri ya kubadwa kwa Mose<br>(ii) Kutetezedwa kwake<br>(iii) Kusamalidwa kwake<br>(iv) Maphunziro ake<br>(v) Udindo umene akanakhala nawo mu Aigupto | Bwerezani phunziro pofunsa mafunso amene akugwirizana kwambiri ndi Phunziro Loyamba.<br>Ganizani za kusamvera lamulo la m'dziko kwa anamwino ndi makolo a Mose. Kambiranani ngati n'koyenera kuti Akhristu azimvera malamulo a dziko ndipo ngati pali nthawi zina pamene kutero kudzakhala kovuta kutero. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Monga momwe Mulungu anayang'anira ndi kutsogolera moyo wa mwana, monga Mulungu anali ndi chikonzero chopambana pa Mose, choncho Iyenso adzayang'anira ndi kutsogolera miyoyo yathu pamene takhulupirira Mwana wake, Ambuye Yesu Khristu, kuti atipulumutse. Kenaka tidzadziwa kuti Mulungu ndiye akulamulira zochitika za miyoyo yathu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Makolo a Mose ndi anamwino anachita zomwe zinali zoyenera chifukwa ankadalira Mulungu ndi kumuopa, ngakhale zinthu zinkaoneka kuti zinali zovuta kwambiri. Kodi ife timakhalabe olimba mtima mu nthawi zovuta kwambiri?<br>2. Tchimo la Mose linadziwika nthawi yomweyo. Mwina titha kuganiza kuti tingathe kubisa "machimo aang'ono", koma adzadziwika ndithu, kaya ndi wina kapena, kufunika kwambiri, Mulungu amene amadziwa zonse. |

| | **B9 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachiwiri – Mose**<br>**Mutu – Cholakwa chake chachikulu** | **B9 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachiwiri – Mose**<br>**Mutu – M’busa wa ziweto** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 2: 11-22***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Numeri 32: 23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mose akufuna kuyamba kuthandiza anthu ake.<br>2. Ife sitingathe kubisa tchimo lathu pamaso pa Ambuye Yesu ngakhale titha kulibisa pamaso pa anzathu.<br>3. Pamene talapa tchimo lathu ndi kuvomereza moona mtima pamaso pa Ambuye Yesu, Iye adzatikhululukira. (Werengani ***1 Yohane 1: 9***) | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 3: 1-16; 4: 1-17***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Machitidwe 7: 35***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu akuonekera kwa Mose ndi kumuwuza kuti abwerere akapulumutse anthu ake.<br>2. Mulungu akulonjeza kukhala ndi Mose pa zimene wamuyitanira kuti akachite. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ophunzira momwe zinathera mu Phunziro Loyamba, Mose anakhala ‘mwana wa mwana wamkazi wa Farao’ ndipo anakulira m’nyumba yaufumu. M’phunziro lino Mose ali ndi zaka makumi anayi ***(Machitidwe 7: 23)*** ndipo akukhudzidwa ndi m'mene ana a Israyeli ankavutikira mu Aigupto. Iye akupha Maigupto ***(Eksodo 2: 12)*** chifukwa cha changu chofuna kuthandiza, koma analakwa pochita tchimo la kupha munthu. Mulungu anali wokonzeka kugwiritsa ntchito Mose yopulumutsa anthu ake, koma ankayenera kudikira zaka zina makumi anayi asanakonzeke kugwira ntchito ya Mulungu! | Fotokozani kwa ophunzira kuti Phiri la Horebe pa ***Eksodo 3: 1*** ndi Phiri la Sinai komanso kuti ndi lofunika kwambiri pa moyo wa Mose.<br>Pa ***Eksodo 3: 12***, Mulungu akuwuza Mose kuti: “Udzapembedza Mulungu pa phiri lino.” Ndi pa phiri limeneli pomwe Mulungu anayankhula ndi Mose ndi kumupatsa ‘Malamulo Khumi’. ***(19: 1-20)*** |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mose ankamva chisoni ndi zomwe zinkachitikira Aisrayeli, koma Mulungu sanakondwe ndi nkhanza zake zakupha Maigupto. Iye akanapemphera kwa Mulungu za zinthu zomwe zinkachitikazo kuti amutsogolere. ***(Eksodo 2: 12)***<br>2. Mose ankaganiza kuti apulumutsa Aisrayeli ndi mphamvu zake, koma ichi sichinali chikonzero cha Mulungu.<br>3. Pamene tchimo lake linadziwika, iye anathawa ndi kupita ku Midyani. ***(2: 15)***<br>4. Pa chitsime ku Midyani anakumana ndi amene adzakhale mkazi wake, Zipora, ***(2: 21)*** ndipo anabereka ana aamuna awiri. Mwana wina ankatchedwa Gerisomu kutanthauza ‘mlendo’. Dzina ili likuonetsa Mose kuti ankadziona kuti ali yekha pamene anali m’dziko la Midyani. Iye anaberekanso mwana wina wamwamuna ndipo anamutcha Eliezere kutanthauza kuti ‘Mulungu ndi thandizo langa’. Mose ankayamika Mulungu chifukwa chomupulumutsa m’manja mwa Farao amene ankafuna kumupha chifukwa anapha Maigupto.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Cholakwa chake chachikulu. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mose anathawira ku Aigupto ndipo tsopano akukhala pakati pa Amidyani. ***(3: 1)***<br>2. Mulungu anayankhula kwa Mose kuchokera m’chitsamba choyaka moto ndipo Mose anavula nsapato zake kusonyeza ulemu. Pamene Mulungu anamuwuza kuti akufuna kumutuma kuti apite kwa Farao kuti akutulutse Aisrayeli mu Aigupto, Mose anafotokoza za kulephera kwake kugwira ntchito imeneyi. ***(3: 10-11)***<br>3. Pakuti Aaigupto anali ndi milungu yambiri, Mulungu anawuza Mose kuti akawuze Aisrayeli kuti ***‘Ine ndine wandituma kwa inu’ (3: 14)*** – Mulungu yekhayo woona ndi wosasintha!<br>4. Mulungu akugwiritsa ntchito ndodo ya Mose ndi kuyisandutsa njoka, kuonetsa Mose mphamvu yake ndi kumuwuza Mose kuti akaonetse mphamvu yomweyi kwa anthu kuti akadziwe kuti Mulungu alipodi. ***(4: 1-5)***<br>5. Potsiriza Mulungu anavomera kuti Aroni azikayankhula m’malo mwa Mose ndipo Mose azikamuwuza Aroni zoyankhula monga Mulungu akumuwuza iye. ***(4: 16)***<br>6. Mose anapita ku Aigupto kuti akayankhule ndi Farao za kumasulidwa kwa Aisrayeli m’dziko la Aigupto. Mwina iyi ndiye inali ntchito yovuta kwambiri m’moyo wake.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – M’busa wa ziweto. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani phunziroli powerenga ***Machitidwe 7: 23-29*** ndipo funsani ophunzira mafunso ogwirizana ndi omwe tafunsa mu Phunziro Lachiwiri kuti atsirize phunziroli. | Jambulani chithunzi cha Mose ndi mabokosi ena olembamo za kukana kwa Mose pamene Mulungu anamuwuza kuti abwerere ku Aigupto akamasule anthu ake a Israyeli. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Kufunika kopempha Ambuye Yesu kuti azititsogolera pamene tikumutumikira komanso kuchita zinthu zoyenera osati molingana ndi maganizo athu.<br>2. Kufunika kwa kusabisa tchimo lathu koma kuvomereza pamaso pa Ambuye Yesu. Kumbutsani ophunzira kuti Mulungu amadziwa zonse; palibe chobisika pamaso pake. | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Mulungu amene anaonekera kwa Mose ndi Mulungu yemweyo amene angakhale m’mitima mwathu ndipo atha kukhala lero. Funsani ophunzira ngati Iye amakhala m’mitima mwawo ndi kulamulira miyoyo yawo.<br>2. Ngati Mulungu atiyitana, kukhala otsatira a Khristu ndi kugwira ntchito yake, Iye adzatithandiza kugwira ntchitoyo monga anachitira Aroni kuyankhula m’malo mwa Mose. |

| | B9 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Mose<br>Mutu – Chitsamba choyaka moto | B9 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Mose<br>Mutu – Mtsogoleri |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 2: 23-25; 3: 1-10***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 15: 11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu ankadziwa kuti ana a Israyeli ankagwira ntchito ngati akapolo ndi mfumu yatsopano ya Aigupto, koma iye ankapita kukawatulutsa kuti apite ku Kanani.<br>2. Mulungu anayitana Mose kuti akatsogolere anthu kutuluka m'dziko la Aigupto kupita ku Kanani. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 7: 1-25***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Miyambo 29: 1***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mphamvu ya Mulungu ndi yoposa mphamvu iliyonse ya munthu kapena bungwe – Iye ndi 'wamphamvuzonse'.<br>2. Anthu ena amapemphera kwa Mulungu akakhala pa mavuto basi ndipo amamuyiwala m'moyo wawo pamene zinthu zawo zikuyenda bwino. |
| MAWU OYAMBA | Kambiranani ndi ophunzira pamene nkhani yafika: Mose wachoka ku Aigupto ndipo wayamba moyo watsopano ku Midyani. Iye alibe maganizo obwerera ku Aigupto, makamaka kwa Farao amene akafuna kumupha. Aisrayeli akuvutika kwambiri mu Aigupto ndipo akulira kwa Mulungu kuti awathandize. Mulungu akuyamba kuyankha pempho lawo kudzera mwa Mose. | Kambiranani ndi ophunzira za momwe Mose ankamvera mu mtima mwake nthawi imeneyi, pamene sankadziwa kuti ku Aigupto akakumana ndi zotani.<br>Tikamachita mantha ndi chinthu china, nthawi zina timafuna chitsimikizo pa zomwe zikuchitikazo, kapena chifukwa chomwe zikuchitika motero ndiponso za amene akutithandiza. Mulungu anachita zimenezi kwa Mose pa ***Eksodo 7: 1-5***. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu anadziwa zomwe ana a Israyeli akukumana nazo – Iye waona, Iye wamva, ndipo anadziwa masautso awo. ***(2: 23-25)***<br>2. Mulungu anamva kulira kwawo ndipo anadziwulula kwa Mose pa Phiri la Sinai, mu chitsamba choyaka moto kuti Iye ndi ndani ndipo za chiyero chake.<br>3. Mulungu anawuza Mose za kukhudzidwa kwake ***(vesi 7)*** ndi ana a Israyeli, momwe Iye adzawapulumutsire m'manja mwa Farao ***(vesi 8)*** ndi kuti adzagwiritsa ntchito Mose kuti awatulutse m'dziko la Aigupto. ***(vesi 10)***<br>4. Kumbutsani ophunzira kuti malo oyamba m'Baibulo pamene pali mawu a opatulika ndi pa ***Eksodo 3: 5*** ndipo povula nsapato Mose akuvomereza kuti pa malo pamene wayimapo ndi 'popatulika'. Tikuyenera kumapereka ulemu kwa Mulungu nthawi zonse.<br>5. Mose adzayenera kuphunzira china chake cha chiyero cha Mulungu, ndi mphamvu zake pamene adzakumana ndi Mulungu pa 'chitsamba choyaka moto'.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Chitsamba choyaka moto. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu anasandutsa Mose kukhala munthu wamphamvu ('Ine ndakuyika kuti ukhale ngati Mulungu kwa Farao' ***(7: 1)*** – woyenera kumveredwa, koma Farao anakana kumvera.<br>2. Mose ndi Aroni anachita zomwe Mulungu anawalamula ndipo pamene Aroni anaponya ndodo yake pansi pamaso pa Farao, inasanduka njoka ndipo pamene amatsenga a Farao anaponya ndodo zawo pansi, zinasandukanso njoka koma ndodo ya Aroni inameza ndodo zawozo, kusonyeza kuti mphamvu ya Mulungu ikugwira ntchito. ***(7: 8-12)***<br>3. Mose ndi Aroni anatambalitsa ndodo yawo pa Mtsinje wa Nailo, ndipo madzi anasanduka magazi. Nsomba zinafa; anthu sanathenso kumwa madzi ake, kuthirira mbewu, kusamba, kapena kupha nsomba. ***(7: 20-21)***<br>4. Farao anakana zomwe Mose ankafuna kuti alole anthu apite.<br>5. Werengani ***chaputala 8-10***, kuti muone miliri ina yambiri imene Mulungu anatumiza kuti Farao amvere ndi kulola Aisrayeli apite. Koma mtima wake unawumitsidwa, ndipo anapitirira kukana. Koma ngakhale Farao anapitiriza kukana, cholinga cha Ambuye pa mapeto chinachitika.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mtsogoleri. |
| KUKUMBUTSANA | Bwerezani phunziro pofotokozera ophunzira nkhani ya pa ***Machitidwe 7: 30-35***. Onetsani ophunzira zomwe Stefano anayankhula za moyo wa Mose ndipo zomwe akunena za chitsamba choyaka moto. | Onani Vesi Yoloweza ndipo kambiranani momwe mukuganizira kuti ikugwirizana ndi phunziro. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ife tikuyenera kukumbukira kuti Mulungu ndi Mulungu woyera, ndipo tikuyenera kumulemekeza ndi kumuopa. Ife tisagwiritse ntchito dzina lake pa chabe monga m'mene anthu ambiri amachitira lero.<br>2. Ngakhale Mulungu ndi woyera, Iye anatumiza Mwana wake, Ambuye Yesu Khristu kudzafera ochimwa ndi kuwakhululukira machimo awo onse, kuphatikiza kusamulemekeza ndi mwano zimene takhala tikumuchitira, ngati tilapa ndi kukhulupirira Mwana wake. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Onani pa ***Salimo 105: 23-29*** ndi kulingalira kuti Mulungu ndiye akulamulira zonse. Ganizirani zotsatira za zimenezi lero pa dziko lapansi.<br>2. Kusandutsa madzi kukhala magazi chinali chodabwitsa koma Mulungu angathe kuchita zambiri ngakhalenso m'miyoyo yathu pamene tikhulupirira Ambuye Yesu ndi ntchito yake ya pa mtanda. |

| | **B9 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Mose**<br>**Mutu – Kubweretsa uthenga wa Mulungu** | **B9 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Mose**<br>**Mutu – Mpulumutsi** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 5: 1-9, 22-23 ndi 6: 1-9***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 10: 31***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mose ndi Aroni anafika pamaso pa Farao ndi kumupempha kuti alole ana a Israyeli kuti apite koma Farao anakana kupereka chilolezo.<br>2. Ambuye anatsimikizira Mose kuti Farao adzalola kuti ana a Israyeli apite chifukwa adzamukakamiza kuti alole kuti apite. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 11: 1-10; 12: 1-13, 21-42***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 1: 29, 1 Akorinto 5: 7***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anabweretsa chiweruzo chake pa Aaigupto chifukwa cha kusamvera kwawo koma anaonetsa chifundo pa Aisrayeli chifukwa cha kumvera kwawo.<br>2. Mwanawankhosa wa Paskha ankalozera imfa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu amene analangidwa chifukwa cha machimo athu mu imfa yake pa mtanda. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani kwa ophunzira kuti ngakhale Mulungu analamula Mose kuti abwerere ku Aigupto, Mose anali ndi mantha chifukwa cha zomwe zidzachitika. Mulungu analonjeza kukhala naye koma Mose sankadziwa kuti Farao adzachita zotani akamuonanso. Choncho Mulungu anawuza Mose kuti m'bale wake Aroni adzamuthandiza. | Dziko lamphamvu la Aigupto sanathe kuletsa Mulungu kuti asakwaniritse malonjezo ake pa Abrahamu ndi Aisrayeli. Mliri wotsiriza uwu unathetsa ukapolo wawo mu Aigupto. Aisrayeli ankayenera kumvera mawu a Mose kuti apulumuke ku chiweruzo cha Mulungu. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pamene anamufunsa kuti alole ana a Israyeli apite, Farao anakana mwa mwano kumvera pempho la Mulungu kudzera mwa Mose ndi Aroni. ***(5: 4)***<br>2. Farao anaonjezera ntchito ana a Israyeli polamula kuti azikapeza okha udzu opangira njerwa. ***(5: 6-7)***<br>3. Mose anayankhula ndi Ambuye pa nkhani imeneyi ndipo Iye anamutsimikizira kuti adzawatulutsa ana a Israyeli m'dziko la Aigupto. ***(5: 22-23, ndi 6: 1)***<br>4. Pa ***Eksodo 6: 6-8***, Ambuye anati, 'Ine ndidza' kasanu ndi akawiri ndipo pa ***Eksodo 6: 2*** anati 'Ine ndine Yehova'. Iye ankafuna Mose ndi Aroni kuti akhulupirire mphamvu yake ndi malonjezo ake. Mulungu anawatsimikiziranso kuti patsala nthawi pang'ono Farao adzaona mphamvu yake pamene adzatumiza zilango khumi (miliri) pa dziko la Aigupto.<br>5. Mose anafotokoza zimenezo kwa anthu a Israyeli, koma iwonso anali okhumudwa ndi opanda mphamvu chifukwa cha ukapolo wawo ndi kuzunzidwa kuti akhulupirire. ***(6: 9)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kubweretsa uthenga wa Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mose ndi Aroni anachenjeza Farao za zimene Mulungu adzachita ngati apitiriza kunyoza mphamvu zodabwitsa zimene Mulungu anachita kudzera mu miliri isani ndi inayi ija. ***(Onani Salimo 105: 26-36)*** Anapereka chenjezo lomaliza. ***(11: 4-6)***<br>2. Anakhazikitsa Paskha, ndipo Aisrayeli analamulidwa kuti awaze magazi a mwanawankhosa mbali ziwiri za khomo la nyumba zawo ndi pamwamba pake.<br>3. Fotokozani kufunika kwa mwanawankhosa; chifukwa chomwe inali nsembe, yolowa m'malo mwa mwana woyamba kubadwa kuti asafe m'nyumbamo. Nyama inkayenera kufa ndi cholinga choti mwana woyamba asafe. ***(12: 1-7)***<br>4. Pakati pa usiku, choopsa chinachitika ndipo mwana aliyense woyamba kubadwa wa Aaigupto anafa koma ana a Israyeli sanafe chifukwa cha magazi a mwanawankhosa amene anawaza m'mbali mwa makomo. ***(12: 29-30)***<br>5. Nthawi imeneyi Farao anavomera kuti anthu a Israyeli apite. Tsopano ulendo wa Aisrayeli wotuluka mu Aigupto unayamba iwo atakhala mu Aigupto zaka 430. Lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu pa ***Genesis 15: 13-14*** linakwaniritsidwa!<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Mpulumutsi. |
| **KUKUMBUTSANA** | Kambiranani zomwe Mulungu wawuza kale Mose ndi momwe anachitira Mose pamene Farao anakana mwachindunji. Pamene Aisrayeli ankayang'ana Mose ndi Aroni ndi kuwaloza zala, m'malo mwake Mose anayang'ana kwa Mulungu ndi kumuloza chala chifukwa cha zimene zinkachitika. Taonani Mulungu ndi wodekha ndi wachifundo ndipo anafotokozanso cholinga chake ndi lonjezo lake kwa iwo: "Ine ndine Yehova". | Limbikitsani ophunzira kuti aganizire tanthauzo la Paskha, kupereka magazi a nyama yosalakwa m'malo mwa Aisrayeli. Kambirananinso kuti inali chizindikiro cha nsembe yayikulu yomwe inkabwera. (Ambuye Yesu anapereka magazi ake kukhala nsembe m'malo mwathu – Iye anali Mwanawankhosa wa Mulungu.) |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Mulungu akufuna kuti ife timvetsetse kuti Iye ndi Mulungu wamphamvuzonse.<br>2. Mulungu akufuna ife timvetsetse za kuopsa kwa kusamvera Iye.<br>3. Mulungu akufuna ife timvetsetse kuti ngakhale mu nthawi zovuta titha nthawi zonse kudalira Iye. Ife tikuyenera kukumbukira kuti Iye sadzatisiya ndi kuti nthawi zonse ali ndi cholinga ndi ife. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi mukudziwa kuti Yesu analipira dipo lalikulu kuti ife timasulidwe ku machimo athu? Kuti Yesu anapereka dipo limeneli kuti atiombole pamene anafa pa mtanda?<br>2. Kodi ife timamuthokoza chifukwa chosenza machimo athu ndi kuthandiza kuti tikhale pa ubale wabwino ndi Mulungu? Chimene tikuyenera kuchita ndi kukhulupirira ndi kulandira mphatso ya moyo wosatha. |

| | **B10 – KALASI 3**<br>**Phunziro Loyamba – Mose**<br>**Mutu – Mwanawankhosa wa Paskha** | **B10 – KALASI 4**<br>**Phunziro Loyamba – Mose**<br>**Mutu – Kuwoloka Nyanja Yofiira** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 12: 1-14, 29-36 ndi 50-51***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 12: 13***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anabweretsa chiweruzo chake pa Aaigupto chifukwa cha kusamvera kwawo ndipo chifundo chake chinaoneka pa Aisrayeli chifukwa cha kumvera kwawo.<br>2. Yesu ndiye anali nsembe yeniyeni ndi Mpulumutsi wathu. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 13: 17-22; 14: 1-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 14: 13***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anali ndi Aisrayeli.<br>2. Aisrayeli anakayikira chitetezo ndi thandizo la Mulungu.<br>3. Mulungu anaonetsa mphamvu yake ndi chikondi chake pa anthu ake powalanditsanso m'manja mwa Aaigupto. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ophunzira kuti aganize za masiku a tchuthi amene timakondwerera ndi zomwe amayimira, monga Khrisimasi ndi Paskha. Fotokozani kuti masiku atchuthi amakhala ofunika kwambiri chifukwa amatikumbutsa zomwe Mulungu anatichitira. Funsani ngati anamva za masiku a tchuthi mu chikhulupiriro cha Chiyuda, monga Paskha. M'nkhani ya lero, tidzaphunzira za Paskha. | Funsani ophunzira kuti aganize kuti ali pa ulendo wautali opita kumene sanapiteko n'kale lomwe.<br>Iwo adzafuna chinthu china (mapu) kapena wina woti awasonyeze njira. Izi ndi zimene Aisrayeli ankafuna pa ulendo wawo wautaliwu wopita ku Dziko la Malonjezano. Mulungu anawatsogolera pa ulendowu m'njira yapadera. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Onaninso ndi ophunzira miliri ya m'mbuyo ndipo fotokozani kuti ukubwera womaliza umene ndi woyipa kwambiri ndi wosakaza. Mulungu adzaonetsa kuti ndi wamphamvu kwambiri kuposa Farao.<br>2. Mulungu anapereka malangizo kwa Mose ndi kwa Aroni zoyenera kuchita. ***(vesi 1-14)***<br>3. Aisrayeli ankayenera kupha mwanawankhosa amene analibe chilema ndi kupaka magazi ake m'mbali mwa makomo awo kuti asafe.<br>4. Fotokozani kufunika kwa mwanawankhosa; momwe inakhalira nsembe, ya kufa m'malo mwa mwana wamwamuna woyamba kubadwa.<br>5. Fotokozani kuti Paskha ndi tchuthi la Ayuda lokumbukira zomwe Ambuye anawachitira "kudutsa" nyumba za amene anapereka nsembe ya nyama. Mwana wamwamuna woyamba kubadwa wa nyumba iliyonse imene inalibe magazi pa khomo lake anaphedwa.<br>6. Fotokozani tanthauzo la Kuomboledwa; kugulanso chinthu chomwe chinali chako / kupulumuka mu ukapolo. Mu Chipangano Chakale, Mulungu ankalandira nsembe za nyama kuchokera kwa wochimwa. Yesu atabwera, Iye analowa m'malo mwathu ndi kupereka moyo wake chifukwa cha machimo athu. Iye ndiye Mpulumutsi wathu – Iye anatiombola ku mphamvu ya tchimo ndi kutibwezeretsa kwa Mulungu. Nsembe ya Yesu inachititsa kuti nsembe ya nyama ikhale yosafunika.<br>7. Potsiriza Farao anavomereza kulola anthu a Israyeli apite - Ambuye asunga lonjezo lake kwa iwo! ***(12: 31-32)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mwanawankhosa wa Paskha. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu anatsogolera Aisrayeli kuchoka mu Aigupto. Iye anawatsogolera kudzera mu chipilala cha mtambo usana ndipo usiku ndi chipilala cha moto. Pamenepo anazindikira kuti Iye anali pakati pawo kuwatsogolera ndi kuwathandiza. ***(13: 21-22)*** *Kambiranani ndi ophunzira kuti nthawi zina anthu amafuna zizindikiro zooneka ndi maso monga ichi kuti adziwe kuti Mulungu ali pakati pawo. Koma Mulungu ali ndi ife tsopano ndipo akutitsogolera kudzera m'Baibulo ndi kudzera mwa Mzimu Woyera - ngati tikumukhulupirira.*<br>2. Ganizirani za mtendere umene Aisrayeli anamva m'mitima mwawo pamene anamasulidwa ku Aigupto. Koma ganizirani momwe mtendere wawo unasandukira mantha pamene anamva kuti gulu la ankhondo a Farao likuwatsatira ndi cholinga choti awabweze! ***(14: 10)***<br>3. Aisrayeli anayamba kuchita mantha ndipo anayamba kuloza zala Mulungu ndi kukwiya. Koma Mose anawakumbutsa kuti akhale bata. Mulungu awamenyera nkhondo. Mose ankaphunzira kudalira Mulungu. ***(14: 13-14)***<br>4. Mulungu anawuza anthu kuti aziyenda ndi kupereka njira yopulumukira pa Nyanja Yofiira kenaka Mulungu anamiza ankhondo onse a Aigupto. Iye anatsekula njira yopulumukira anthu ake. Mulungu anachita chodabwitsa ichi polekanitsa nyanja pofuna kuonetsa mphamvu yake ndi chikondi chake pa anthu ake. ***(14: 21-28)***<br>5. Aisrayeli anapereka ulemu waukulu kwa Mulungu ndipo tsiku limenelo anakhulupirira Iye ndi Mose. ***(14: 31)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuwoloka Nyanja Yofiira. |
| **KUKUMBUTSANA** | Atakhala mu ukapolo kwa zaka zambiri ndi kulira kwa Mulungu, patabwera miliri yambiri ndiponso Farao atakana kumvera Mulungu, anthu a Israyeli anali afulu tsopano! Kambiranani pa gulu kuti iwo anamva bwanji m'mitima mwawo pamene ankachoka mu Aigupto. | Funsani mafunso ophunzira kuchokera pa phunziro la lero monga njira yobwereza phunziroli. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi inu mukudziwa kuti dipo lalikulu linaperekedwa kuti ife timasulidwe ku tchimo lathu? Kuti Yesu anapereka dipo ndi kutiombola pamene anafa pa mtanda?<br>2. Kodi ife timathokoza chifukwa chotenga machimo athu ndi kutithandiza kuti tikhale pa ubale wabwino ndi Mulungu? Chimene ife tikuyenera kuchita ndi kumukhulupirira ndi kulandira mphatso yake ya moyo wosatha. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Pamene zinthu sizikuchitika m'mene timaganizira kapena momwe timayembekezera, ife tichite chiyani? Kodi timaloza chala Mulungu ndi kukwiya naye? Kapena timakumana ndi mavutowo ndi chitsimikizo kuti Mulungu atithandiza ngati tikumudalira, ngakhale osati m'njira imene ife timaganizira kapena kuyembekezera?<br>2. Kambiranani kuchokera pa phunziro ili kuti Mulungu ndi Mulungu wa zatheka bwanji. (Onani pa ***Yesaya 43: 2-3***) |

| | **B10 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachiwiri – Mose**<br>**Mutu – Nyanja Yofiira** | **B10 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachiwiri – Mose**<br>**Mutu – Pa Phiri la Sinai** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 13: 20-22; 14: 5-14, 19-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 14: 14***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anapulumutsa anthu ake osankhika m'dziko la Aigupto.<br>2. Aisrayeli anayamba kukayikira Mulungu ndi chisamaliro chake pa iwo.<br>3. Mulungu anali pakati pawo kuwatsogolera ndi kuwateteza. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 19: 1-13, 16-25; 20: 1-21***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 19: 5 ndi 20: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu ndi woyera ndi wamphamvu.<br>2. Ife tili ndi mwayi ofika pamaso pa Mulungu mosavuta, zomwe Aisrayeli sakanatha.<br>3. Mulungu anapereka kwa Aisrayeli malangizo a momwe akuyenera kukhalira. |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani zomwe Aisrayeli ankamva mu mtima mwawo. Monga mtundu anakhala mu Aigupto zake 430 ali mu ukapolo ndipo tsopano akhala afulu. Funsani ophunzira afotokoze zomwe akuganiza kuti Aisrayeli ankaganiza nthawi imeneyi. | Ganizani zochitika za tsiku ndi tsiku pamene timakhala ndi malamulo ndi malangizo, monga malangizo akagwiritsidwe ka ntchito ka chinthu kapena malangizo amaphikidwe. Ndondomeko zimenezi zilipo kuti zitithandize ife.<br>Zinalinso chomwecho ndi Malamulo Khumi amene Mose analandira kuchokera kwa Mulungu kupita kwa anthu a Israyeli. Anaperekedwa kuti awathandize kutsogolera zochita zawo. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br><br>1. Potsiriza Aisrayeli anali afulu ndipo ali pa ulendo opita ku Dziko la Malonjezano kutali ndi dziko la Aigupto! Ganizirani za chisangalalo chawo kuti tsopano amasulidwa mu ukapolo!<br>2. Mulungu anatsogolera Aisrayeli kudzera mu chipilala cha mtambo usana ndi chipilala cha moto usiku. ***(13: 21-22)*** Izi zinasonyeza kuti nthawi zonse anali pakati pawo ndipo ankawatsogolera. *Nthawi zambiri, timafuna titakhala ndi zizindikiro zooneka ndi maso kuti Mulungu ali pakati pathu. Koma Iye atha kutitsogolera ndi kutithandiza kudzera m'Baibulo ndi kudzera mwa Mzimu Woyera.*<br>3. Pamene gulu la ankhondo a Farao linayamba kutsatira Aisrayeli, Aisrayeli anachita mantha kwambiri ndi kudandaula kuti Mulungu sankawateteza. Iwo sanamukhulupirire. ***(14: 10-11)*** Iwo anali atayiwala momwe Mulungu anawathandizira ndi kuwafikitsa pamenepo. *Fotokozani kuti nthawi zambiri timakhala ndi maganizo amenewa zinthu zikakhala kuti sizikuyenda bwino m'miyoyo yathu.*<br>4. Mose anali ndi bata ndi maganizo abwino pa nthawi imeneyi ndipo anakumbutsa anthu kuti Mulungu adzawamenyera nkhondo. ***(14: 14)***<br>5. Mulungu anaonetsa mphamvu yake pogawa Nyanja Yofiira pakati kuti Aisrayeli adutse ndi kuononga ankhondo a Aigupto m'madzimo pamene Aisrayeli anaoloka mpaka tsidya lina. ***(14: 21-22, 26-28)***<br>6. Aisrayeli anawopa Ambuye ndipo anamukhulupirira Mose monga mtsogoleri wawo. ***(14: 31)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Nyanja Yofiira. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Patha miyezi iwiri kuchokera pamene Mulungu anatulutsa Aisrayeli mu Aigupto. Iye akuwathandiza kukonzekera zomwe zikubwera patsogolo pawo. ***(19: 1)***<br>2. Mulungu anawuza Mose kuti awuze anthu kuti iwo ndi osankhidwa ake ndi kuti ndi chuma cha pamtima pake. ***(19: 5-6)*** Iye anawawuza kuti aziyeretse. *Fotokozani tanthauzo la kudziyeretsa – kudzipatula, kukhala a ukhondo pa thupi ndi mu mzimu kukonzekera kukumana ndi Mulungu.*<br>3. Aisrayeli sankayenera kukhudza phiri chifukwa linali lopatulika. Mphamvu ya Mulungu ndi chiyero chake zinali za mphamvu kwambiri kuti anthu samuyandikire Iye. ***(19: 10-13)*** *Kambiranani za kusangalatsa kwa kuti lero titha kufika mwaufulu pamaso pa Mulungu woyera ameneyu, Mulungu wamphamvu, chifukwa cha zonse zimene anachita Ambuye Yesu.*<br>4. Mulungu analola Mose yekha kuti afike pamaso pake ndipo anamupatsa Malamulo Khumi. ***(20: 1-17)*** Malamulo amenewa anawuza anthu a Israyeli udindo wawo kwa Mulungu ndi kwa wina ndi mnzake. Anaperekedwa kuti atsogolere Israyeli kukhala moyo wachiyero komanso kuti aone khalidwe la Mulungu ndi kukonza miyoyo yawo.<br>5. Anthu anachita mantha ndipo sanafune kukwera phiri, choncho Mose anakhala m'khalapakati pa iwo ndi Mulungu. Wina wamkulu kuposa Mose, Yesu, ndiye anakhala M'khalapakati yekhayo wa pakati pa Mulungu ndi mtundu wa anthu. ***(1 Timoteo 2: 5)***<br>6. Mose akuwawuza kuti asachite mantha koma kuti mantha a Ambuye adzakhala pakati pawo. Mantha awo anali choopsa. Mose ankafuna kusinthanitsa ndi mantha a Ambuye amene amabweretsa kudalira ndi kumvera ndiponso amachititsa anthu kuti asamachimwe. ***(20: 20)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Pa Phiri la Sinai. |
| **KUKUMBUTSANA** | Jambulani zithunzi za nkhani iyi: Mulungu akutsogolera Aisrayeli, Aisrayeli akuzindikira kuti Aaigupto akuwatsatira ndi m'mene Mulungu anawapulumutsira. | Bwerezani phunziro pofunsa ophunzira kuti atchule Malamulo Khumi ndipo mukambirane lililonse. Kodi tingatsatire motani Malamulowa m'miyoyo yathu? |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Zinthu zoyipa zikachitika pa miyoyo yathu, kodi timaloza chala Mulungu ndi kumanena kuti zachitika chifukwa Mulungu sali nafe kapena sakufuna kutithandiza? Kapena ife timakhala ngati Mose amene akukhulupirira kuti Mulungu watithandiza ndipo adzapitirira kutithandiza ndi kutimenyera nkhondo, ngati tingamudalire? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Tikaganizira momwe Aisrayeli ankachitira mantha ndi za kusayenera kwawo kufika pamaso pa Mulungu, kodi ife tikumvetsa za mwayi umene tili nawo ofika mwaufulu chifukwa cha Yesu Khristu pamaso pa Mulungu? Ife tikuyenera kumuyamika chifukwa chosenza machimo athu kuti tikhale oyera pamaso pa Mulungu. (Onani pa ***2 Akorinto 5: 21***) |

| | B10 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Mose<br>Mutu – Ulendo wovuta | B10 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Mose<br>Mutu – Kutuluka m'moto |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 17: 1-16***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Petro 5: 7***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Aisrayeli anapitirira kukayikira Mulungu.<br>2. Mulungu sanawakhumudwitse ndipo anapitiriza kuwapatsa zosowa zawo ndi kuwamenyera nkhondo. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 32: 1-35***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 32: 26 ndi 33***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Anthu a Israyeli anayiwala msanga Malamulo a Mulungu.<br>2. Mulungu anachitira chifundo amene ankamutsatira ndi kulanga amene sankamutsatira. |
| MAWU OYAMBA | Onani kutali kumene Aisrayeli achokera ndi momwe Mulungu wakhalira akuwapatsa zosowa zawo, miliri mu Aigupto, kugawa madzi pa Nyanja Yofiira. Funsani ophunzira kuti afotokoze zomwe Aisrayeli ankaganiza za Mulungu mpaka pamenepa. | Funsani ophunzira kuti aganizire nthawi yomwe ankachita chinthu chomwe ankadziwa kuti chinali cholakwika. Ganizirani kuti ndi chifukwa chiyani nthawi zambiri timavomera kutsatira gulu m'nyengo izi. Mu phunziro lino tiphunzira kuti sitikuyenera kukhala monga Aroni koma monga Mose ndi kutsatira njira za Mulungu. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Aisrayeli anayambanso ulendo wawo, kutsatira kulamula kwa Ambuye. Koma panalibe madzi oti amwe pa ulendo wawo. Choncho iwo anayamba kudandaulanso. ***(17: 2-3)*** Iwo anadandaulira Mose m'malo mopemphera kwa Mulungu ndi kumudalira.<br>2. Mulungu anawathandiza mwakukoma mtima kwake, posaganizira za kung'ung'udza kwawo, ndi madzi otuluka pa thanthwe – Iye sakuwakhumudwitsa koma akuchita chodabwitsa! ***(17: 5-6)***<br>3. Mavuto sanathe chifukwa Amaleki anabwera kudzawathira nkhondo! ***(17: 8)*** Anthu awa ankadziwika kuti anali oyipa mtima, owopsa amene kupha anthu kunali ngati masewero. *Ganizirani momwe Aisrayeli ankamvera mu mtima atachoka ku Aigupto ndipo tsopano akukumana ndi mavuto onsewa ofuna kuphedwa ndi Amaleki!*<br>4. Koma Mulungu anawathandiza. Mose anayima pamwamba pa phiri ndi kukweza m'mwamba ndodo ya Mulungu. Ndodo akayikweza m'mwamba, iwo ankapambana koma akayitsitsa ankagonja! Mosatenga nthawi, manja a Mose anatopa, choncho Aroni ndi Huri anamuthandiza kutukula manja ake m'mwamba. ***(17: 11-13)***<br>5. Tsiku limeneli Aisrayeli anapambana nkhondo – Mulungu anali pakati pawo kuwathandiza kugonjetsa m'dani ameneyu. Izi zikusonyeza kuti Mulungu adzatsogolera anthu ake kudzera mwa Mose.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Ulendo wovuta. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Anthu a Israyeli anaona ngati Mose akuchedwa kutsika m'Phiri la Sinai. Iwo anaganiza zoti achite pofuna adzithandiza, motero anapanga mulungu wawo. Iwo anachotsa utsogoleri wa Ambuye ndi kukhazikitsa utsogoleri wa fano limene ankatha kulilamula. Kambiranani kuti kutero kunali kuswa malamulo awiri oyamba. ***(32: 1-4)***<br>2. Mulungu ataona zimene zinkachitika, Iye anali wokonzeka kuononga mtundu wonse chifukwa cha kusamvera kwawo ***(32: 10)*** koma Mose anadandaulira Mulungu kuti asachite zimenezi. Mulungu akuonetsa chifundo pamenepa. ***(32: 11-14)*** *Fotokozani tanthauzo la chifundo (kupulumuka ku chilango chokuyenerani).*<br>3. Mose anatsika phiri ali wokwiya kwambiri chifukwa cha anthuwo ndipo anaphwanya mwala umene panali Malamulo Khumi uja pamaso pawo, kufuna kuwaonetsa kuti aswa malamulo a Mulungu. ***(32: 19)*** Koma Mulungu anali wokwiya kwambiri kuposa Mose chifukwa cha anthuwa.<br>4. Mose anakhumudwa ndi Aroni chifukwa anatsogolera Israyeli kusochera. Iye akanadziwa kuti zomwe anthu ankafuna kuchita zinali zolakwika koma m'malo mwake iye anamvera madandaulo awo ndipo anawathandiza kupanga mwana wang'ombe wagolide woti azimupembedza. ***(32: 21-22)***<br>5. Mose anafunsa Aisrayeli kuti, "Kodi ndani ali mbali ya Ambuye?" Aliyense amene sanayankhe ndi kutsatira Mulungu anaphedwa tsiku limenelo. ***(32: 26-29)*** *Kumvera Mulungu ndi kofunika kwambiri kuposa kumvera kwina kulikonse.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kutuluka m'moto. |
| KUKUMBUTSANA | Phunzirani Vesi Yoloweza ndi kukambirana pagulu zomwe iwo angachite. Kumbukirani kuti Mulungu akufuna kuti tizimudalira nthawi zonse. | Onani pa ***1 Yohane 5: 21*** ndi kuganiza kuti ndi mtundu wanji wa "fano" umene ungatenge malo a Mulungu m'miyoyo yathu. Gwiritsani ntchito vesi iyi ndi "mafano" awa kupanga chojambula cha pa khoma choonetsa kufunika kwa kutsatira ndi kumvera Mulungu. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi nthawi zina timayiwala kuti Mulungu angathe kutithandiza mu nyengo zathu zovuta? Ife tikuyenera kumakumbukira kupita kwa Iye kuti atithandize kumenya nkhondo zathu komanso mu nyengo zathu zonse zovuta.<br>2. Ganizirani momwe Aroni ndi Huri anathandizira Mose kukweza manja ake m'mwamba – iwo anamulimbikitsa ndi kumuthandiza. Kodi ife tingathandize anzathu motani lero? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Nthawi zambiri timalakwitsa ndi kukhala osamvera Mulungu. Koma titha kukhululukidwa ndi Mulungu tikalapa ndi kumupempha.<br>2. Aroni sanachite chomwe ankadziwa kuti chinali chabwino. Kodi tingaganizepo nthawi imene ife timachita zimenezi ndi kutsatira zofuna za gulu? Tipemphere kuti Mulungu atithandize kumumvera kuti tisagonjere mayesero pamene takumana nawo. |

| | **B10 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Mose**<br>**Mutu – Njoka yamkuwa** | **B10 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Mose**<br>**Mutu – M'chipululu** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Numeri 21: 4-9, Yohane 3: 1-2, 14-16***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 3: 14-15***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Aisrayeli anadandaulanso kwa Mulungu.<br>2. Mulungu ankayenera kuwalanga – KOMA anakonza njira yoti apulumukire ku chilango chawo.<br>3. Ichi chinali chithunzi cha zomwe zidzachitika m'tsogolo pamene Yesu adzapachikidwa pa mtanda chifukwa cha machimo athu. | **Ndime Yowerenga:** ***Numeri 21: 1-9***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 3: 14-15***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Aisrayeli anayiwala msanga momwe Mulungu anawasamalira ndi kuwapatsa zosowa zawo mpaka pamenepa.<br>2. Mulungu ankayenera kuonetsa anthu a Israyeli momwe ankachimwira ndi kusamudalira kwawo.<br>3. Mulungu anapereka njira yopulumukira ku chilango chawo. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ophunzira za nthawi imene ankaona kuti zinthu zomwe ankazidikira zikuchedwa kapena wina akuchedwa kukwaniritsa lonjezo lake. Fotokozani kuti Mulungu anali atalonjeza kale Aisrayeli Dziko la Malonjezano, koma iwo ankaona kuchedwa kufika m'dzikolo. | Kambiranani za kuyenda ulendo wautali. Nthawi zambiri, anthu amaona kuchedwa ndipo amatopa ndi ulendo, makamaka ana. Nthawi zina amafuna atafika ku maloko msangamsanga.<br>Umu ndi m'mene Aisrayeli ankamvera mu mtima za kufika ku Dziko la Malonjezano limene Mulungu anawawuza. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nthawi imeneyi Aisrayeli anali atakhala m'chipululu zaka makumi anayi ndipo anayamba kutaya mtima. Iwo anayankhula motsutsana ndi Mulungu – "Chifukwa chiyani munatitulutsa kuchoka m'dziko la Aigupto kuti tidzafere m'chipululu muno?!" ***(Numeri 21: 4)***<br>2. Choncho Mulungu anakwiya chifukwa chosamudalira. Iye anatumiza njoka zaululu kwambiri pakati pawo ndipo ambiri anafa. Koma Mose anapemphera kwa Mulungu m'malo mwa anthuwo kuti awakhululukire. ***(21: 7)***<br>3. Mulungu anawuza Mose kuti apange njoka yamkuwa ndi kuyipachika pa mtengo ndipo aliyense akalumidwa ndi kuyang'ana njokayo adzachira. Njoka yamkuwa inathandiza kuti Aisrayeli achire. Akayang'ana, ndiye kuti Aisrayeli ankavomereza kuti chilango ndi chochokera kwa Mulungu, kusonyeza kuti ndi Mulungu yekha amene angawapulumutse. ***(21: 9)***<br>4. Aisrayeli sanazindikire kuti njoka imene inali pa mtengoyo inali ndi tanthauzo lina lalikulu. Pa ***Yohane 3***, Yesu akufotokoza kuti monga Aisrayeli ankachiritsidwa akayang'ana njoka imeneyi, moteronso lero titha kuchiritsidwa ku tchimo lathu tikayang'ana pa imfa ya Yesu pa mtanda. Sinali njoka imene inawachiritsa koma chikhulupiriro chawo ndiye chinawachiritsa.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Njoka yamkuwa. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nthawi imeneyi Aisrayeli anali atakhala m'chipululu zaka makumi anayi ndipo anayamba kutaya mtima. Mulungu anawalonjeza Dziko la Malonjezano, koma iwo sankaliona dzikolo. Motero, iwo anayamba kudandaula ndi kung'ungu'udza motsutsana ndi Mulungu chifukwa cha nyengo zawo, m'malo mokumbukira kumene Mulungu anawatenga. ***(Numeri 21: 4-6)***<br>2. Izi zisanachitike, iwo anakumana ndi nyengo zambiri zoopsa, koma Mulungu anakwaniritsa zosowa zawo ngakhale kuti iwo anali ndi moyo wopanda chikhulupiriro ndi moyo odandaula.<br>3. Koma tsopano Mulungu anakwiya nawo ndipo anawatumizira njoka za ululu kwambiri zomwe zinkaluma anthuwo ndipo ambiri anafa. ***(21: 6)***<br>4. Mosachedwa anthu anazindikira tchimo lawo ndipo anafunsa Mose kuti apemphe Mulungu kuti awakhululukire. ***(21: 7)***<br>5. Choncho, Mulungu analangiza Mose kuti apachike pa mtengo njoka yamkuwa ndipo amene adzayang'ana njokayo adzakhala ndi moyo. Poyang'ana njoka, iwo ankavomereza kuti Mulungu ndiye anatumiza chilango ichi ndipo ndi Mulungu yekha amene anatha kuwapulumutsa. ***(21: 9)***<br>6. Anthu a Israyeli sanazindikire ichi, koma ichi chinali chifaniziro cha Ambuye Yesu pa mtanda. Iwo amene ankayang'ana njokayo, ululu wawo unkachoka ndipo sankafa. M'njira yomwe, iwo amene amayang'ana kwa Ambuye Yesu pa mtanda ndi kumukhulupirira sadzafa koma adzakhala ndi moyo wosatha. (Onani Vesi Yoloweza)<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – M'chipululu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Funsani ophunzira kuti aone vesi yodziwika bwino, ***Yohane 3: 16*** ndi kukambirana tanthauzo la moyo wosatha. Anthu sakondwa ndi maganizo a moyo wosatha chifukwa chosakondwera ndi miyoyo yawo ya dziko lapansi. Koma moyo wosatha umene Yesu akupereka ulibe matenda, imfa, zoyipa kapena tchimo! Pamene tadziwa Khristu ndi kumutsatira, izi zimasintha m'mene timaonera moyo pa dziko lapansi. | M'magulu ang'onoang'ono, onani ndi kuphunzira ***Salimo 78: 10-38*** ndi kulemba zodabwitsa zonse zimene Mulungu anachitira anthu ake ndiponso khalidwe lawo kwa Iye ndi zimene Iye anachita. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Aisrayeli anadandaula motsutsana ndi Mulungu chifukwa sankamudalira. Iwo sankamvera malamulo ake ndiponso anayiwala zonse zimene anawachitira m'mbuyomo. Kambiranani zinthu zimene ife timadandaula zomwe zimabwera chifukwa cha zochita zathu ndi makhalidwe athu. Ife tikuyenera kuthetsa kudandaula kwathu kuti kusalamulire miyoyo yathu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Anthu a Israyeli anadandaula pamaso pa Mulungu za nyengo zomwe ankakumana nazo, ngakhale kuti Iye sanawakhumudwitsepo. Nthawi zambiri, ife timakhala ngati iwo ndipo timayiwala madalitso ambiri amene Mulungu amatipatsa ndi kuti adzatisamalira ngati tingamudalire. Kodi ife tinayang'ana kwa Yesu pa mtanda, kumukhulupirira kuti atipulumutse ku machimo athu ndi kutipatsa moyo wosatha? |

| | B11 – KALASI 3<br>Phunziro Loyamba – Mose<br>Mutu – Kukumana ndi Mulungu | B11 – KALASI 4<br>Phunziro Loyamba – Lamulo<br>Mutu – “Mulungu m’modzi” |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 19: 1-14***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Petro 1: 16***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu ndi woyera ndi wangwiro.<br>2. Kumvera ndi kofunika kwambiri pa ubale wathu ndi Mulungu.<br>3. Malamulo a Mulungu amaonetsera uchimo mwa anthu. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 19: 16-25; 20: 1-7, Mateyu 22: 34-40***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 22: 37***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu ndi Mulungu woyera<br>2. Mulungu ndi Mulungu wamphamvu.<br>3. Mulungu ndi Mulungu wa nsanje.<br>4. Mulungu ndi Mulungu wa chikondi. |
| MAWU OYAMBA | Funsani ophunzira kuti aganizire zomwe angachite ngati akupita ku ukwati, monga kuchapa zovala, kusamba ndi kuonetsetsa kuti mwavala bwino chifukwa cha tsiku lalikulu! Fotokozani momwe anthu a Israyeli anachitira zimenezi pokonzekera kukumana ndi Mulungu chifukwa Iye ndi wangwiro ndi wopanda tchimo pamene anthu a Israyeli anali ochimwa. | M’phunziro lino, tikambirana momwe Mulungu analamula anthu a Israyeli kuti asakhale ndi milungu ina kapena mafano koma Iye yekha. Ngati chinthu china chibwera pakati pa ife ndi Mulungu, limenelo ndi fano.<br>Ganizirani za mafano kapena milungu pakati pathu lero ndi kukambirana ndi ophunzira momwe zimakhalira m’malo a Mulungu m’miyoyo yathu. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mose yekha ndiye anatha kupita ku phiri kukakumana ndi Mulungu. Kupezeka kwa Mulungu kunali kwa mphamvu kwambiri ndi kopatulika, motero anthu a Israyeli sakanatha kupita kwa Iye. ***(vesi 3)***<br>2. Mulungu anali ndi chifukwa chopulumutsira Aisrayeli kuchoka mu ukapolo m’dziko la Aigupto ndipo tsopano akuwawuza. Iye akufuna kuti iwo azimumvera ndi kumutsatira. Mulungu ankafuna kuti Israyeli ukhale mtundu wopatulika, anthu ake osankhidwa. ***(vesi 5-6)***<br>3. Atamva malamulo a Ambuye anayankha kuti adzachita zonse zimene Ambuye adzanena. ***(vesi 8)***<br>4. Mulungu anawuza Mose kuti ayeretse anthu a Israyeli kuti amupembedze. ***(vesi 10)*** Uku kunali kukonzekera kuti akumane ndi Mulungu. Iwo ankayenera kusamba ndi kukonza mitima yawo ndi maganizo awo kuti akumane ndi Mulungu. Fotokozani kwa ophunzira momwe kudziyeretsera ku thupi kukanawathandizira kukonzekeranso m’maganizo kuti akhale oyera pamene akupembedza Mulungu.<br>5. Onani Vesi Yoloweza kuti mudziwe chifukwa chomwe ankayenera kukonzekera kuti akumane ndi Mulungu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukumana ndi Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Aisrayeli afika pa Phiri la Sinai ndipo akukonzekera kuti apite akakumane ndi Mulungu. Mulungu ndi woyera kwambiri n’chifukwa chake iwo ankayenera kudziyeretsa okha. ***(19: 14)***<br>2. Mulungu anatsika Kumwamba maonekedwe a moto – anthu a Israyeli ananjenjemera chifukwa cha mantha pansi pa mphamvu yake. ***(19: 16-18)***<br>3. Mulungu anawuza anthu kuti asakhale ndi mulungu wina koma Iye yekha. ***(20: 3)*** Iye anawawuzanso kuti asapembedze milungu ina kapena mafano, chinthu chimene chingatenge malo ake. Iye ndi Mulungu wa nsanje ndi chikondi chathu, ndipo Iye akulonjeza chikondi chopanda malire kwa amene amamukonda Iye ndi kusunga zolamulira zake. ***(20: 5-6)***<br>4. Mulungu akanena kuti ndi wa nsanje, nsanje yake sili ngati ya munthu yomwe ndi yoyipa. Nsanje ya Mulungu imaonetsa chikondi chenicheni ndi kukhudzidwa pa munthu.<br>5. Iwo sankayenera kugwiritsa ntchito dzina la Ambuye pachabe. M’mene timagwiritsira ntchito dzina lake zimasonyeza momwe timaganizira za Iye. Ife tigwiritse ntchito dzina lake lopatulika potamanda ndi kupembedza, osati pamene tikuyankhula zosayenera kapena kulumbira. ***(20: 7)***<br>6. Yesu ali pa dziko lapansi, atsogoleri a Malamulo ankafuna kumupezera cholakwa. Funsani ophunzira kuti aone pa ***Mateyu 22: 34-40***. Kodi molingana ndi Yesu lamulo lalikulu ndi liti?<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – “Mulungu m’modzi”. |
| KUKUMBUTSANA | Kambiranani ndi ophunzira chomwe chikuchititsa kuti Phiri la Sinai likhale lopatulika. Apa Iye anayankhula ndi Mose pa chitsamba choyaka moto ***(Eksodo 3: 1-12)***. Mulungu anayankhulanso kwa Eliya m’kamphepo ka kayaziyazi pamene anathawa kufuna kupulumutsa moyo wake. ***(1 Mafumu 19: 1-13)*** | Phunzirani Vesi Yoloweza ndi kukambirana pa gulu momwe vesiyi ikufotokozera phunziro lonse la lero mwachidule. Funsani mafunso amene adzathandiza kuti atsirize phunziro loyamba. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Mulungu ndi woyera ndi wangwiro ndipo ife ndife ochimwa kwambiri ndi odetsedwa moti tikufunika kupeza njira yoti tithe kufika pamaso pake.<br>2. Ichi ndi chifukwa chomwe Mulungu anatumizira Mwana wake Yesu pa dziko lapansi kuti adzatifere: kuti tikhululukidwe machimo athu. Pamene takhulupirira Ambuye Yesu, Mulungu amatitenga kukhala oyeretsedwa ndi oyera! | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Funsani ophunzira kuti akambirane ngati m’miyoyo yawo muli zina zomwe zatenga malo a Mulungu kapena n’zofunika kuposa Mulungu? Mwina akambirane za kufunika kwake.<br>2. Kambiranani ngati amagwiritsa ntchito dzina la Mulungu pachabe kapena kulumbira. Izi zimamvetsa chisoni Mulungu. Limbikitsani ophunzira kuti aganizire mosamala momwe iwo amagwiritsira ntchito dzina la Mulungu. |

| | B11 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Mose<br>Mutu – Kudziwa Mulungu | B11 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Lamulo<br>Mutu – “Njira ya Mulungu” |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 20: 1-12***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 22: 37***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu ndi Mulungu m’modzi woona.<br>2. Dzina la Mulungu ndi lopatulika ndipo likuyenera kulemekezedwa.<br>3. Tsiku Lamulungu ndi lapadera ndipo tizipuma.<br>4. N’kofunika kwambiri kulemekeza amayi ndi abambo athu. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 20: 8-11, Luka 13: 10-17***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 20: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu akufuna ife tisunge tsiku la Sabata monga tsiku lopatulika.<br>2. Kusunga malamulo kusalepheretse ife kukonda anthu. |
| **MAWU OYAMBA** | Ganizani zochitika za tsiku ndi tsiku pamene malamulo ndi chinthu chabwino. Mwa chitsanzo: pa masewero, makolo kuletsa ana kukhudza chinthu chotentha, maloboti a pa msewu, nthawi yogona, kupita ku sukulu ndi zina zambiri. Kambiranani ndi ophunzira momwe Mulungu anaperekera malamulo kwa anthu a Israyeli kuti akhale mtundu wake wopatulika - Malamulo Khumi. Iwo ankafuna chitsogozo cha Mulungu kuti akhale moyo umene Mulungu ankafuna. | Ganizirani zochitika za tsiku ndi tsiku pamene malamulo ndi ofunika kwambiri monga pa masewero, makolo akuletsa ana kuti asagwire chinthu chotentha, maloboti a pa msewu, nthawi yogona, kupita ku sukulu ndi zina zambiri. Kambiranani ndi ophunzira momwe Mulungu anaperekera Malamulo Khumi kwa Israyeli kuti akhale mtundu wake wopatulika ndi kuwaonetsa khalidwe labwino kuti akhale pansi pa chitetezo chake. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Lamulo Loyamba ***(vesi 1-3)*** limene Mulungu anapereka linali loti asakhale ndi milungu ina kapena mafano koma Iye yekha. Fano ndi chilichonse chimene chimatenga malo a Mulungu m’miyoyo yathu. Izi zinali zofunika kwambiri kwa Mulungu; n’chifukwa chake lili Lamulo Loyamba. Yesu anatsimikiza izi pa ***Mateyu 4: 10.***<br>2. Lamulo Lachiwiri ***(vesi 4)*** linali loti asapange mafano aliwonse. Izi zitha kuoneka ngati zosavuta, koma anthu a Israyeli anali atangochoka ku Aigupto, kumalo kumene kunali mafano ambiri ndi milungu yambiri. Yesu akutsindika Lamulo ili pa ***Luka 16:13***.<br>3. Lamulo Lachitatu ***(vesi 7)*** linali loti asagwiritse ntchito dzina la Ambuye Mulungu wathu pachabe. Dzina la Mulungu ndi lapadera ndipo tisaligwiritse ntchito molakwika. M’mene timagwiritsira ntchito dzina lake zimaonetsa zomwe timaganiza za Iye. Tigwiritse ntchito dzinali potamanda ndi kupembedza osati poyankhula zolakwika kapena kulumbira.<br>4. Lamulo Lachinayi ***(vesi 8-11)*** linali loti azisunga Sabata kukhala tsiku lopatulika, losiyana ndi masiku ena asanu ndi limodzi a pa sabata. Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi masiku asanu ndi limodzi ndipo anapuma tsiku la Sabata, ndipo ife tikuyenera kutsatira zomwe Iye anachita. Mulungu amafuna tizikhala ndi tsiku lopuma kuti tizimupembedza ndi kumuyamika chifukwa cha chilengedwe chake.<br>5. Lamulo Lachisanu ndi chimodzi ***(vesi 12)*** linali lolemekeza abambo ndi amayi awo. *Kambiranani tanthauzo la kulemekeza ndi momwe ife tingalemekezere makolo athu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kudziwa Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Limodzi mwa Malamulo Khumi kwa Aisrayeli linali losunga tsiku la Sabata kukhala lopatulika, lodzipereka kwa Mulungu. ***(Eksodo 20: 8-11)***<br>2. Mulungu mwini analenga kumwamba ndi dziko lapansi masiku asanu ndi limodzi ndipo anapuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Iye akutilimbikitsa ife ndi kuti tizichita zomwezo ndi kuti tizikhala ndi tsiku limodzi pa sabata losiyana ndi masiku ena, lopuma ndi lopembedza Mulungu ndi kumuyamika chifukwa cha chilengedwe chake. ***(Genesis 2: 2)***<br>3. Mulungu anali atayamba kale kuwaonetsa Aisrayeli zoyenera kuchita kudzera m’malangizo ake pamene ankatenga mana. ***(Eksodo 16: 22-26)***<br>4. Pamene Yesu anali pa dziko lapansi, anthu sankakondwera ndi m’mene Iye “akasungira” lamulo ili. Iwo ankanena kuti akuswa lamuloli akachiritsa anthu odwala pa tsiku la Sabata. Izi zinachitika nthawi zambiri. Nkhani imodzi ikupezeka pa ***Luka 13: 10-17.***<br>5. Yesu anawadzudzula chifukwa cha chinyengo chawo pakuti iwo ankatha kusamalira ziweto zawo pa tsiku la Sabata, koma Yesu ndiye asasamalire anthu ake? Iwo anasokonekera m’Malamulo ndipo posunga Malamulo anayiwala zomwe Mulungu ankafuna pa miyoyo yawo. ***(Luka 13: 15-17)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – “Njira ya Mulungu”. |
| **KUKUMBUTSANA** | Onani pa ***Mateyu 22: 37-40*** ndi kukambirana momwe mavesi awa akufotoza Malamulo Khumi onse mwachidule. Funsani mafunso kuti athandize ophunzira kutsiriza Phunziro Lachiwiri. | Ophunzira akambirane za kusunga Sabata m’magulu awiri; “Losunga” ndi “Lokana”. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Kodi ife timayika milungu ina kapena mafano patsogolo kuposa Mulungu? Ife tikuyenera kuonetsetsa kuti zinthu zina monga masewero, TV, ntchito ndi zina zambiri zisatenge malo a Mulungu m’miyoyo yathu.<br>2. Kodi timalumbira kapena kugwiritsa ntchito dzina la Mulungu m’njira yolakwika? Ife tikuyenera kusamala ndi dzina la Mulungu chifukwa ndi lapadera ndi lopatulika.<br>3. Kodi timatenga tsiku Lamulungu kukhala lapadera kwa ife kusiyana ndi masiku ena onse?<br>4. Kodi timalemekeza abambo athu ndi amayi athu? | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Palibe aliyense wa ife amene angasunge Malamulo onse; ndife ochimwa ndipo sitingakwaniritse zofuna za Mulungu pa tokha. ***(Aroma 3: 23)***<br>2. Ife sitingakondweretse Mulungu poyesetsa kusunga Malamulo amenewa.<br>3. Yesu Khristu anabwera kuti ife tikhale pa ubale wabwino ndi Mulungu, komanso kudzalangidwa chifukwa cha tchimo lathu. Ife tikamulandira m’miyoyo yathu, Iye amapereka Mzimu Woyera kuti atithandize kukhala moyo woyenera. |

| | **B11 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachitatu – Mose**<br>**Mutu – Kumvera Mulungu** | **B11 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachitatu – Lamulo**<br>**Mutu – “Mulungu akhale woyamba”** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 20: 13-21, Mateyu 19: 16-30***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 19: 21***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anapereka Malamulo awa kuti tiziwasunga.<br>2. Kumvera Malamulo amenewa, sizitanthauza kuti tidzakhala ndi moyo wosatha.<br>3. Ife titha kuyika zinthu zina m’miyoyo yathu m’malo mwa Mulungu. | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 20: 12-21, Marko 10: 17-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 6: 24***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Zolamulira ndi malamulo ndi zofunika kuti tizimvera.<br>2. Zolamulira ndi malamulo pa zokha sizingabweretsa ubale wabwino ndi Mulungu kapena moyo wosatha.<br>3. Ife titha kuyima mafano mosavuta m’malo mwa Mulungu. |
| **MAWU OYAMBA** | Ganizirani zomwe timachita pofuna kumvera malamulo a pa sukulu, koma nthawi zina timayiwala ndi kuphwanya malamulowo. Taperekani zitsanzo. Fotokozani kuti timachita izi chifukwa ndife anthu ochimwa ndipo sitingathe kukhala angwiro ngati Mulungu. | Ganizira momwe timayesetsa kutsatira malamulo ku sukulu, koma nthawi zina timayiwala ndi kuphwanya. Perekani zitsanzo. Fotokozani kuti izi zimachitika chifukwa ndife anthu ochimwa ndipo sitingakhale angwiro ngati Mulungu. Ife palibe chimene tingachite kuti tikalowe Kumwamba. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Lamulo Lachisanu ndi Chimodzi linali loti tisaphe. Onani pa ***Mateyu 5: 21-22*** kuti muone tanthauzo latsopano la Yesu pa za kupha munthu. *Kambiranani momwe zikutikhudzira lero pa ubale wathu ndi anthu ena.*<br>2. Lamulo Lachisanu ndi Chiwiri linali loti tisachite chigololo.<br>3. Lamulo Lachisanu ndi Chitatu linali loti tisabe. Mu Chipangano Chatsopano, Yesu akufotokozanso izi ndipo akuti ngati munthu aba malaya anu, inu mupatseninso mkanjo wanu! ***(Mateyu 5: 40)***<br>4. Lamulo Lachisanu ndi Chinayi linali loti tisapereke umboni wonama wa mnansi wathu. Fotokozani kwa ophunzira kuti kutero ndi kunena zabodza za wina kapena kusanena nkhani yonse monga m’mene inachitikira. *Onani pa **Mateyu 12: 36** kuti muone zomwe Yesu anayankhula pa nkhani imeneyi.*<br>5. Lamulo la Khumi linali loti tisasirire kapena kuchita nsanje ndi zomwe ena ali nazo. Kufuna kuti zonse zikhale zako ndi kupanda chikhulupiriro pa Mulungu monga wokwaniritsa zosowa zathu.<br>6. Werengani ***Mateyu 19: 16-30*** pamodzi ndi ophunzira. Kambiranani momwe Yesu akufotokozera kuti kusunga malamulo onse sizikutanthauza kuti ukalandira moyo wosatha. Chipulumutso sichibwera chifukwa cha ntchito zabwino zokha koma pakuyenera kukhala mtima wokonda Mulungu, ndiponso wofuna kusiya zonse ndi kukhulupirira Ambuye Yesu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kumvera Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi, Iye anali kukwaniritsidwa kwa Lamulo komanso kusintha kwathunthu kwa Malamulo ena. ***(Mateyu 5: 17-18)***<br>2. Lamulo Lachisanu - lemekeza abambo ako ndi amayi ako – ***Mateyu 10: 37*** akuonetsa maganizo atsopano a Yesu pa lamulo limeneli.<br>3. Lamulo Lachisanu ndi Chimodzi – usaphe. Onani pa ***Mateyu 5: 21-22*** kuti mupeza tanthauzo la Yesu pa nkhani ya kupha munthu. *Kambiranani momwe izi zikukhudzira anthu lero.*<br>4. Lamulo Lachisanu ndi Chiwiri – usachite chigololo. Mu ***Mateyu 5: 27-28*** tikuona momwe Yesu akufotokozera.<br>5. Lamulo Lachisanu ndi Chitatu – usabe. Yesu akufotokozanso limeneli. ***(Mateyu 5: 40)***<br>6. Lamulo Lachisanu ndi Chinayi – usachite umboni wonama kutsutsa mnansi wako. Fotokozerani ophunzira kuti kutero ndi kuyankhula zonama pa zimene wina anachita kapena kusiya zina zomwe wina anachita. *Onani pa **Mateyu 12: 36** kuti muone zomwe Yesu ananena pa lamulo limeneli.*<br>7. Werengani ***Marko 10: 17-31***. Kambiranani momwe Yesu akuonetsera kuti chipulumutso sichibwera chifukwa cha ntchito zabwino koma n’kofunika kukonda Mulungu, mtima wofuna kusiya chuma chonse ndi kukhala ndi chikhulupiriro mwa Yesu yekha.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – “Mulungu akhale woyamba”. |
| **KUKUMBUTSANA** | M’magulu ang’onoang’ono, ganizira zinthu zimene zingakhale m’miyoyo yathu zomwe zingakhale zofunika kwambiri kuposa Mulungu, zomwe zimatilepheretsa kutenga Mulungu kukhala woyamba. Kambiranani zomwe tingachite kuti tichotse zinthu zimenezo, kulola kuti Mulungu akhale woyamba m’miyoyo yathu. (Onani pa ***Mateyu 6: 33***) | Pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi, Iye anali wosintha zinthu mwamphamvu. Iye anaphunzitsa kuti ntchito zabwino ndi kusunga malamulo sizinali zokwanira. Yesu anadzipereka kukhala nsembe kuti machimo athu akhululukidwe. Chomwe ife tikuyenera kuchita ndi kudalira ndi kukhulupirira kuti Iye anatifera basi. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Kodi tikuganiza kuti tikakhala abwino ndi omvera makolo, aphunzitsi ndi zina zambiri, Mulungu adzakondwera nafe ndipo tidzakhala ndi moyo wosatha? Werengani ***Aefeso 2: 8-9***.<br>2. Kodi ife tidzalakwitsa monga m’mene mnyamata wachuma anachitira pamene anapita kwawo ali ndi chisoni chifukwa sanafune kusiya zina kuti m’moyo mwake mukhale Mulungu? | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Kodi ife tili ngati mnyamata wachuma uja poganiza kuti ndife abwino kwambiri chifukwa timasunga malamulo onse? Kusunga malamulo ndi chinthu chabwino koma sikutipatsa moyo wosatha kapena ubale ndi Mulungu.<br>2. Ife timalandira moyo wosatha pamene takhulupirira Yesu osati chifukwa cha zomwe timachita. Ambuye Yesu ndi njira yokhayo kukafikira kwa Mulungu. ***(Yohane 14: 6)*** (Onaninso ***Aefeso 2: 8***) |

| | B11 – KALASI 3<br>Phunziro Lachinayi – Mose<br>Mutu – Kukhumudwitsa Mulungu | B11 – KALASI 4<br>Phunziro Lachinayi – Lamulo<br>Mutu – “Mawu a Mulungu” |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Eksodo 32: 1-26***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Eksodo 32: 26***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Anthu a Israyeli anabwerera m’mbuyo ndi kuyamba kusamvera Mulungu.<br>2. Mulungu anaonetsa chifundo kwa amene anamutsatira ndipo analanga amene sanamutsatire. | **Ndime Yowerenga:** ***Marko 7: 1-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Timoteo 1: 15 ndi Aroma 5: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Afarisi anali achiphamaso.<br>2. Miyambo sinkayenera kukhala yofunika kuposa Mawu a Mulungu.<br>3. Yesu analimbikitsa otsatira ake kuti akhale ndi mitima yoyera. |
| MAWU OYAMBA | Funsani ophunzira aganize nthawi imene anawauza kuti asachite kanthu.... Koma iwo anachimwabe! Kodi zotsatira zake zinali chiyani? Fotokozani kuti izi ndiye zinachitika apa ndipo anthu a Israyeli anayiwala Mulungu ndipo anayambanso kupembedza milungu yawo yabodza. | Ganizirani za miyambo yomwe tili nayo, mwina m’mabanja mwathu kapena mu mpingo. Ina itha kukhala yabwino ndipo ina itha kukhala yoyipa. Miyambo yabwino imagwirizana ndi Mawu a Mulungu ndi kutilimbikitsa kutumikira ndi kumvera Iye. Koma isakhale yofunika kuposa Mawu a Mulungu. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Anthu a Israyeli anataya mtima pamene ankadikira Mose uku atsike ku Phiri la Sinai. Choncho iwo anapanga milungu yabodza kuti azipembedza. ***(32: 1-4)*** Iwo anafuna kukhala ndi fano lawo limene akanalipanga okha ndi kumalilamulira. Iwo anali atayiwala kale Malamulo awiri oyamba aja. ***(Eksodo 20:1-5)***<br>2. Mulungu anali wokonzeka kuononga mtundu wonse chifukwa cha kusamvera kwawo ndi tchimo lawo ***(32: 10)*** koma Mose anapempha Mulungu kuti asachite zimenezi. Mulungu akuonetsa chikondi chake ndi chifundo apa posawaononga onse. *Fotokozani tanthauzo la chifundo (kusalangidwa pamene uli woyenera kutero).*<br>3. Mulungu anaonetsa chifundo kwa amene anali ofuna kutsatira Ambuye ***(32: 26)*** koma ena anaphedwa chifukwa cha kusamvera kwawo.<br>4. Mose anakhumudwa ndi Aroni chifukwa chotsogolera anthu a Israyeli kusochera. Iye ankayenera kudziwa kuti zomwe anthu a Israyeli ankachita zinali zolakwika koma m’malo mwake anamvera madandaulo awo ndi kuwathandiza kupanga mwana wang’ombe wagolide kuti azimupembedza. ***(32: 22-24)*** *Kodi ife nthawi zina timachita zinthu zomwe tikudziwa kuti ndi zolakwika chifukwa cha kuti aliyense akuchitanso?*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukhumudwitsa Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nthawi imene Yesu anali pa dziko lapansi, Malamulo amene Mose ndi anthu a Israyeli anapatsidwa ankagwirabe ntchito. Koma anaonjezera miyambo imene inali ndi malamulo ndi malangizo ambiri, osachokera kwa Mulungu, a makhalidwe a anthu.<br>2. Afarisi anali ndi mtima oweruza ena, choncho anabwera kudzaona zomwe Yesu ankachita. Iwo anadzudzula ophunzira a Yesu chifukwa cha zimene anachita, kunena kuti ankaphwanya malamulo a Mulungu. ***(Marko 7: 5)***<br>3. Afarisi anali anthu achiphamaso. Zochita zawo zinali za kunja kokha, kuti aliyense aone ndipo sizinkachokera mu mitima imene inali kutali ndi Mulungu. Iwo ankapembedza ndi zifukwa zolakwika; chifukwa ankafuna kumaoneka ngati oyera kuti anthu aziwapatsa ulemu. ***(Marko 7: 6-8)***<br>4. Yesu anadzudzula Afarisi chifukwa cha kusamvera kwawo Malamulo a Mulungu, chifukwa cha malamulo awo amene anakhazikitsa, monga kusasamalira amayi ndi abambo. Iye anadzudzula kwambiri chifukwa chosunga malamulo ndi miyambo yawo kuti aoneke ngati oyenera m’malo mopereka ulemu kwa Mulungu. ***(Marko 7: 9-13)***<br>5. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake za kufunika kwa mtima woyera ndi momwe zoyipa ndi makhalidwe a uchimo amatulukira m’miyoyo yathu ngati sitifunafuna mtima woyera. ***(Marko 7: 17-23)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – “Mawu a Mulungu”. |
| KUKUMBUTSANA | Funsani ophunzira mafunso a nkhani ya lero ngati njira yobwereza phunziro ndi kuwathandiza kuti atsirize. | Funsani ophunzira kuti aone pa ***Marko 7: 21-22*** ndi kufananitsa ndi ***Afilipi 4: 8***. Kambiranani makhalidwe amene akuyenera kukhala m’miyoyo yathu ndi m'mene tingakhalire motero. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Monga Mulungu anachitira chifundo Aisrayeli ngakhale anachimwa, Iye lero athanso kuchitira chifundo ife ngati tinamupempha kuti atikhululukire zolakwa zathu zimene tachita.<br>2. Mulungu ndi Mulungu wachikondi ndipo safuna kuti atilange chifukwa cha machimo athu. N’chifukwa chake anatumiza Mwana wake kudzatifera kuti ife tisadzalangidwe chilango chotiyenera. Pamene tikhulupirira Ambuye Yesu titha kukhululukidwa. | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>1. Ife tisafulumire kuweruza ndi kudzudzula anthu popanda kuganizira kaye za m’mene moyo wathu ulili ndi zolinga zathu. ***(Mateyu 7: 1-2)***<br>2. Monga Afarisi, ife tisakodwe m’malamulo athu ndi miyambo yathu ndi kuona ngati ndi m’mene tikuyenera kukhalira. Kuchita izi kutha kutilepheretsa kupereka ulemu kwa Mulungu. Ngati tikukayika, tiyenera kupempha Ambuye Yesu kuti atitsogolere pa makhalidwe athu. |

| | **B12 – KALASI 3**<br>**Phunziro Loyamba – Chimwemwe cha Khrisimasi!**<br>**Mutu – Malonjezo a Mulungu** | **B12 – KALASI 4**<br>**Phunziro Loyamba – Chimwemwe cha Khrisimasi!**<br>**Mutu – Mwana wamwamuna wabadwa** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Yesaya 9: 1-7, Mika 5: 2***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yesaya 9: 6***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kubadwa kwa Yesu kunaloseredwa zaka zambiri m'mbuyomo Iye asanabadwe.<br>2. Anthu ambiri ankadikira ndi chiyembekezo za kubadwa kwa Yesu.<br>3. Yesu ndi Mesiya amene anthu anakhala akumudikira kwa nthawi yayitali, Kuunika kwa dziko lapansi. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 1: 26-38; 2: 1-7***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 1: 35***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kubadwa kwa Yesu kunali kukwaniritsa maulosi amene analembedwa zaka zambiri za m'mbuyomo.<br>2. Mariya ndi Yosefe anali ofuna kuti Mulungu awagwiritse ntchito pa chikonzero chake pa dziko lapansi.<br>3. Kubadwa kwa Yesu sikunadziwike mu Betelehemu. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ophunzira ngati akudziwa mayi aliyense amene anali woyembekezera. Afotokozereni kuti miyezi isanu ndi inayi ndi yomwe mayi amadikira kuti abereka mwana wake. Aneneri anafotokozera anthu a Israyeli za kubwera kwa Yesu koma iwo anadikira zaka zambiri Iye asanabadwe. | Kambiranani ndi ophunzira momwe mungakonzekere zinthu monga tchuthi, phwando kwa tsiku lobadwa, maukwati, kukacheza ndi anzathu. Kambiranani zomwe timachita pamene chikonzero chathu chasokonekera kapena kulephereka kuchitika monga m'mene tinakonzekera. Kambiranani za chikonzero cha Mariya choti akwatiwe Yosefe, koma Mulungu anali ndi cholinga chachikulu pa iye ndi Yosefe. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kambiranani ndi ophunzira za kuti sitidziwa kuti agoletsa zigoli zingati mpaka mpira utatha, kapena zomwe tidzakhala tikuchita zaka makumi anayi zikubwerazo. Ife sitingathe kulosera. Koma Yesaya ndi Mika analosera za kubwera kwa Yesu pa dziko lapansi zaka zambiri m'mbuyomo Iye asanabadwe.<br>2. Mneneri Yesaya akunena za anthu amene ali mu mdima waukulu kuti adzaona kuwala kumene kudzawalira onse amene ali mu mdima. ***(Yesaya 9: 2)*** Funsani ana kuti aone pa ***Yohane 8: 12*** kuti adziwe kuunika ndi ndani.<br>3. Funsani ana aone pa ***Mateyu 4: 14-16*** kuti aone kukwaniritsidwa kwa maulosi a mu Yesaya patapita zaka zambiri.<br>4. Kambiranani ndi ana momwe chikonzero chachikulu cha chipulumutso cha dziko lapansi chinali chodabwitsa ndi momwe Ayuda anadikirira zaka zambiri kuti chikonzerochi chikwaniritsidwe. Ambiri sanakhale moyo mpaka kuona kubadwa kwake. Kambiranani za kupambana kokhala ndi mbiri yonse ya moyo wa Yesu m'Baibulo kuti ife tithe kumudziwa kuti Iye ndiye Mpulumutsi wathu.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Malonjezo a Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu anatuma mngelo kuti adzawuze Mariya kuti adzakhala ndi mwana. Mariya akuchita mantha chifukwa ndi namwali ndipo sakudziwa kuti izi zidzatheka bwanji. Koma mngelo anamutsimikizira ndi kumuwuza kuti wapeza chisomo pamaso pa Mulungu. ***(Luka 1:26-34)***<br>2. Mwina Mariya sanamvetse zomwe zinkachitika koma ankadziwa kuti akuyenera kukhulupirira Mulungu. ***(1: 38)*** Kambiranani zomwe tingachite titamva nkhani imene idzasintha kwambiri miyoyo yathu mpaka muyaya.<br>3. Pamene Mariya ali wotopa kwambiri, Mariya ndi Yosefe ananyamuka ulendo opita ku Betelehemu kuchokera ku Nazarete kuti akachite kalembera. Kalembera uyu analamula ndi Augusto. ***(Luka 2: 1-5)*** Kambiranani momwe Augusto ankaganizira kuti iye ndiye ankalamulira zochitika, komatu anali Mulungu ndipo ili linali gawo limodzi la chikonzero chake kuti Ambuye Yesu abadwire ku Betelehemu.<br>4. Yesu anabadwira mu Betelehemu kukwaniritsa ulosi wa Mika. ***(Mika 5: 2)*** *Kambiranani kufunika koti Yesu ankakwaniritsa maulosi.*<br>5. Yesu atabadwa, Mariya anamukulunga m'nsalu ndi kumugoneka modyera ng'ombe. ***(2: 7)***<br>6. Kambiranani momwe Ayuda ankadikirira Mfumu yawo yolonjezedwa kuti ibwere mwaulemero wachifumu, koma Yesu anabadwa pakati pa ziweto. Fotokozani kuti sitikuyenera kumupatsa malire Mulungu ndi kuganiza kuti zidzachitika monga m'mene tikuganizira. Iyi inali mbali imodzi ya chikonzero cha Mulungu pa Yesu. Iye ankatsogolera Mariya ndi Yosefe ndi kukwaniritsa zonse zimene ankazifuna. Werengani ***2 Akorinto 8: 9.***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mwana wamwamuna wabadwa. |
| **KUKUMBUTSANA** | Werengani ***Yesaya 9: 6 ndi 7*** pamodzi ndi ophunzira ndi kukambirana za dzina lililonse limene Yesaya analemba lofotokoza za Yesu. Kambiranani ndi ophunzira kuti mupeze kuti Yesu adzatchedwa bwanji mayina onsewo. | Funsani ophunzira kuti adzifanizire kuti iwo ndi Mariya kapena Yosefe. Afunseni alembe zochitika ngati Mariya kapena Yosefe molingana ndi zowachitikira zomwe taphunzira m'phunziroli. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Funsani ana kuti aganize za khalidwe la kuunika ndi chifukwa chomwe chidzachititsa Yesu kutchedwa kuunika kwa dziko lapansi. ***(Yesaya 9: 2)***<br>2. Thandizani ana kuti aone Yesu monga kuunika kwa dziko lapansi. Pamene tikuona zounikira pa nthawi ya Khrisimasi, mwina zidzatikumbutsa kuti Yesu ndi Kuunika Kwenikweni, kotumizidwa ku dziko lapansi kudzatipulumutsa mu mdima ndi ku chilango chifukwa cha tchimo lathu.<br>3. Ophunzira alembe kalendala ya kubwera kwake yokhala ndi mayina osiyana a Yesu pa tsiku lililonse mpaka tsiku la Khrisimasi. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kambiranani ngati ophunzira ndi okonzeka ngati Mariya kuvomereza chikonzero cha Mulungu pa miyoyo yawo, ngakhale kuti atakhala kuti sakumvetsetsa.<br>2. Kodi ife tikuchita chiyani ndi Yesu amene anthu anamudikirira nthawi yayitali? Kodi ife timangomuona ngati khanda modyera ng'ombe pa nthawi ya Khrisimasi? Kapena kuti Iye ndi Mpulumutsi amene akufuna kukhala m'miyoyo yathu tsiku ndi tsiku? |

| | B12 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Chimwemwe cha Khrisimasi!<br>Mutu – Kudabwa kwa Mariya! | B12 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Chimwemwe cha Khrisimasi!<br>Mutu – Kulengeza za Mpulumutsi |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 1: 26-38***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 1: 32***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Maulosi onena za Yesu anakwaniritsidwa kuonetsa kuti ili linali gawo lofunika pa chikonzero cha ulamuliro wa Mulungu.<br>2. Ife, monga Mariya ndi Yosefe, timakhala ndi zikonzero zathu koma chikonzero cha Mulungu pa miyoyo yathu ndiye chimapambana. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 2: 8-20***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 2: 11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Angelo a Kumwamba anali osangalala ndi za kubwera kwa Mesiya, Khristu.<br>2. Abusa aziweto anali osangalala kukumana ndi Yesu ali khanda atamva mawu ochokera kwa angelo.<br>3. Ife tikuyeneranso kukhala osangalala ndi kukondwerera kubadwa kwa Yesu. |
| MAWU OYAMBA | Kambiranani ndi ophunzira momwe mungakonzekere nthawi ya tchuthi, tsiku lobadwa, ukwati, kukacheza ndi anzathu. Kambiranani zomwe tingachite ngati chikonzero chathu chitasokonekera kapena osakwaniritsa zomwe ife timafuna kuti zichitike. Kambiranani momwe Mariya ndi Yosefe ankakonzekerera zoti akwatirane koma Mulungu anali ndi chikonzero china chachikulu pa iye ndi Yosefe. | Ganizirani momwe amalengezera mwana akabadwa, makolo ena amalemba kadi kapena kutumiza zithunzi za mwanayo. Pamakhala chisangalalo ndi chimwemwe. Fotokozani kuti Yesu sanali ngati mwana wamba choncho anthu salengeza za kubadwa kwake! Kumbukirani kuti Iye anabwera kwa anthu wamba, motero abusa aziweto ndiye anali oyamba kudziwa za kubadwa kwake. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mulungu anatumiza mngelo Gabrieli kwa Mariya kukamuwuza kuti adzakhala ndi mwana ngakhale kuti sanakwatiwe. ***(vesi 26-31)***<br>2. Mariya akuvutika mu mtima ndipo sakumvetsa zomwe zidzachitike, koma mngelo akumutsimikizira kuti wapeza chisomo pamaso pa Mulungu ndi kuti palibe chosatheka ndi Mulungu. ***(vesi 34-37)*** *Kambiranani ndi ophunzira tanthauzo la zimenezi.*<br>3. Fotokozani mfundo zofunika za kuti Mariya anali wochokera ku Galileya ndipo Yosefe anali mwana wa Davide. Kambiranani ndi ophunzira chifukwa chomwe izi zili zofunika; aneneri anati Mesiya amene akubwerayo adzachokera ku Galileya ***(Yesaya 9: 1)*** ndipo adzakhala mwana wa Davide. ***(Yesaya 9: 7)*** Fundo izi zinali gawo limodzi la chithunzi chachikulu chokwaniritsa maulosi onse.<br>4. Mwina Mariya sanamvetsetse zomwe zinkamuchitikira, koma iye anadziwa kukhulupirira Mulungu. ***(vesi 38)*** Kambiranani zomwe tikanachita titamva nkhani ngati imeneyi yomwe idzasintha kwathunthu moyo wathu mpaka kalekale.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kudabwa kwa Mariya. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Usiku umene Yesu anabadwa, abusa aziweto ankayang'anira ziweto zawo ku tchire. Fotokozani kuti kuyang'anira nkhosa usiku kumakhala kuli bata moti mwina abusawo amagona tulo. ***(vesi 8)***<br>2. Koma usiku umenewo china chake chodabwitsa chinachitika! Mngelo anaonekera kwa iwo ndipo onse anachita mantha! *Funsani ophunzira kuti iwo akanamva bwanji m'mitima mwawo.* ***(vesi 9)***<br>3. Mngelo anabwera kudzawawuza kuti Yesu, Mpulumutsi, wabadwa. ***(vesi 11)***<br>4. Kenaka kunaoneka angelo ambiri ndipo ankayimba nyimbo zotamanda Mulungu, kukondwerera kubwera kwa Ambuye Yesu pa dziko lapansi. *Fotokozani kukongola kwa maonekedwe awo kuti kunali kotani kwa abusa amene anali mu mdima ndi nkhosa zawo.* ***(vesi 13-14)***<br>5. Angelo atachoka, abusa anafulumira kupita kuti akaone mwanayo okha. *Kambiranani zomwe ankamva m'mitima mwawo nthawi imeneyi; mwina iwo ankaganiza kuti anali maloto chabe kapena angelo sankanena zoona.*<br>6. Iwo anapeza mwana monga m'mene angelo anafotokozera! ***(vesi 16)*** Iwo anatamanda ndi kukweza Mulungu ndipo kenaka anayamba kufotokozera aliyense za Mpulumutsi amene wabadwa. ***(vesi 17 ndi 20)***<br>7. Ganizirani za kusangalala kwa abusawa pamene anaona mwanayo ndi kuti nthawi yomweyo anayamba kufotokozera anthu za Iye ndi kuyamba kugawana ndi ena Nkhani Yabwino imeneyi.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kulengeza za Mpulumutsi. |
| KUKUMBUTSANA | Lembani malonjezo onse amene mngelo Gabrieli akunena mu Vesi Yoloweza. Kodi tikuphunzira chiyani kuchokera m'vesi imeneyi za Mfumu imene ikubwerayo ndi zomwe yabwera kudzachita? Kodi ife timakhulupirira kuti malonjezo amenewa akunena za Yesu? | Pangani posita kapena lembani pa khoma momwe mukuganizira kuti ndiye ankalengezera za kubadwa kwake. Muphatikize zomwe angelo ananena (Vesi Yoloweza) pa zomwe mwapangazo. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ndife okonzeka ngati Mariya kuvomereza chikonzero cha Mulungu pa miyoyo yathu, ngakhale titakhala kuti sitikumvetsetsa?<br>2. Kodi ife tikanachita chiyani ndi Yesu amene anthu anakhala akumudikira nthawi yayitali?<br>3. Kodi ndife ofuna kudalira Ambuye ndi tsogolo lathu, ngakhale kuti mwina zinthu sizidzachitika monga tikufunira? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ndife osangalala ngati abusawa kuti titha kuwuza ena nkhani ya Yesu? Kodi mukuganiza kuti kubadwa kwake kunali kopatsa chidwi kuti achite m'mene iwo anachitiramo?<br>2. Kodi ife timasangalala pa Khrisimasi pa zifukwa zoyenera? Kodi ndi nkhani yopatsana mphatso ndi kudyerera kapena timasangalala za kubwera kwa Yesu pa dziko lapansi kuti adzakhale Mpulumutsi wathu? |

| | B12 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Chimwemwe cha Khrisimasi!<br>Mutu – Kubadwa kwa Yesu | B12 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Chimwemwe cha Khrisimasi!<br>Mutu – Kupembedza Ambuye |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** *Luka 2: 1-7*<br>**Vesi Yoloweza:** *2 Akorinto 8: 9*<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kubadwa kwa Yesu sukunadziwike mu Betelehemu<br>2. Yesu, Mwana wa Mulungu anali munthu ndithu.<br>3. Ulosi wa kubadwa kwake unalembedwa zaka zambiri m'mbuyomo. | **Ndime Yowerenga:** *Mateyu 2: 1-12*<br>**Vesi Yoloweza:** *Mateyu 2: 11*<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pamene Yesu ankabadwa ena anamulandira pomwe ena sanamulandire.<br>2. Mulungu ankayang'anira Yesu, Mariya ndi Yosefe kuti atetezedwa. |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani ndi ophunzira zomwe akanachita ngati mfumu kapena mfumukazi akubwera kudzakuchezerani kwanuko; mwina anthu atha kukhala osangalala kwambiri ndi kuchita zikondwerero zopambana! Koma pamene Yesu anabadwa, palibe amene anadziwa. Kunja kunali zii. Kunalibe malo ngakhale m'nyumba za alendo kuti afikiremo, koma Iye malo ake anali modyera ng'ombe. | Funsani ana kuti aganizire zomwe timachita mwana akabadwa. Kambiranani za kugula mphatso ndi kupita kumunyamula mwanayo. Fotokozani kuti iyi ndi nthawi ya chisangalalo! |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mariya ndi Yosefe akuyenera kuchoka ku Nazarete ndi kupita ku Betelehemu kuti achite kalembera; kuti akawerengedwa ndi kulembetsa mu kaundula. Kambiranani za kutopetsa kwa ulendo wautali umenewu kwa mayi woyembekezera, makamaka m'masiku amenewa. ***(vesi 1-4)***<br>2. Amene analamula kalembera ameneyu ndi Augusto. *Kambiranani momwe Augusto ankaganiza kuti ndi iye amene anaganiza za kalembera, koma osadziwa kuti anali Mulungu ndipo iyi inali mbali imodzi ya chikonzero chake.*<br>3. Pamene anali kumeneko, Yesu anabadwa m'mene munali ziweto ndipo anamugoneka modyera ng'ombe. ***(vesi 7)***<br>4. Yesu anabadwira ku Betelehemu pokwaniritsa ulosi wa kuti Mesiya adzabadwira ku Betelehemu. ***(Mika 5: 2)*** *Kambiranani za kufunika koti Yesu akwaniritse maulosi ofunikawa.*<br>5. *Kambiranani momwe kubadwa kotere si m'mene mfumu imabadwira, koma ichi chinali chikonzero cha Mulungu pa Ambuye Yesu. Iye ankatsogolera Mariya ndi Yosefe ndi kuwapatsa zonse zofunikira.*<br>6. *Kambiranani za kuti Ayuda ankadikirira mfumu yawo kwa nthawi yayitali kuti ifike mwa ulemerero, koma Yesu anabadwira pakati pa ziweto. Fotokozani kuti sitikuyenera kumuyikira malire Mulungu ndi kuyembekeza kuti zinthu zichitika monga tikuganizira.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kubadwa kwa Yesu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mfumu Herode ndiye anali mfumu pamene Yesu anabadwa.<br>2. Anzeru a kum'mawa anayenda ulendo kuchokera Kum'mawa chifukwa nyenyezi inawawuza kuti ibadwa mfumu yatsopano. Iwo anafunsa Mfumu Herode kuti mfumuyi inali ndani. ***(vesi 1-2)***<br>3. Mfumu Herode inavutika mu mtima ndi nkhaniyi, kuti padzakhala mfumu ina amene adzatenga malo ake. Izi zinali chomwechi chifukwa iye sanali mfumu ya Israyeli yovomerezeka, monga m'mene analili Ambuye Yesu. Iye anali ankakayikira 'mfumu' imeneyi. ***(vesi 3)***<br>4. Iye anawuza anzeru a kum'mawa kuti apite ndipo akakapeza mfumuyo akabwerenso kuti iyenso adzapite kukamulambira. Koma Herode ankakonza zofuna kumupha mwanayo. ***(vesi 7-8)***<br>5. Anzeru a kum'mawa anatsatira nyenyezi mpaka anapeza nyumba imene munali mwanayo. Nthawi imeneyo mwina n'kuti ali ndi chaka chimodzi kapena ziwiri pamene iwo ankafika. Pamene anamuona Iye, anasangalala kwambiri! Iwo anamupembedza ndi kumupatsa mphatso za golide, lubani ndi mure. ***(vesi 10-11)***<br>6. Mulungu anawuza anzeru aja m'maloto kuti adzere njira ina pobwerera kwawo kupewa Mfumu Herode chifukwa ankafuna kupha Yesu. Iwo anamvera Mulungu ndipo anasintha njira kuti ateteze Yesu. ***(vesi 12)***<br>7. *Siyanitsani zomwe anachita anzeru a kum'mawa ndi zochita za Herode. Iwo anazindikira kuti Yesu ndi Mesiya, Mpulumutsi wa dziko lapansi, pamene Herode anaona Yesu ngati chiopsezo cha mpando wake waufumu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kupembedza Ambuye. |
| **KUKUMBUTSANA** | M'magulu ang'onoang'ono, lembani nkhani yoti mutumize ku nyuzi pepala ya ku Betelehemu yolengeza za kubadwa kwa Yesu. | Funsani mafunso ophunzira pa phunziro la lero ngati njira yobwereza phunziroli ndi kuwathandiza Phunziro Lachitatu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Anthu sanazindikire Yesu pamene ankabadwa chifukwa sankadziwa za Iye. Ife timadziwa za Iye tsopano, koma timamuzindikira? Kodi timangomuona ngati khanda m'modyera ng'ombe nthawi ya Khrisimasi? Kapena kodi Iye ndi Mpulumutsi amene ife tikuyenera kukhala moyo chifukwa cha Iye tsiku ndi tsiku?<br>2. Yesu anakhala munthu ndi cholinga choti akafe pa mtanda chifukwa cha machimo athu. Kodi ife timamvetsetsa za chikonzero chopambana cha chipulumutso cha Mulungu? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ife tili ngati anzeru a kum'mawa a m'nkhaniyi? Kodi timafunafuna Ambuye Yesu kuti timupembedze ndi kumupatsa mphatso? Kapena timayembekezera kuti Iye atipatse mphatso ndi kutithandiza pamene ife palibe chomwe tikumupatsa?<br>2. Iwo amene ndi 'anzeru' amafunafuna Yesu lero kuti amupembedze osati chifukwa cha zomwe angalandire kuchokera kwa Iye koma chifukwa cha chimene Iye ali. |

| | **B12 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Chimwemwe cha Khrisimasi!**<br>**Mutu – Uthenga wa mngelo** | **B12 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Chimwemwe cha Khrisimasi!**<br>**Mutu – Chipulumutso!** |
|---|---|---|
| | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 2: 8-20***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 2: 11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Angelo a Kumwamba anali osangalala ndi nkhani yakubwera kwa Ambuye Yesu, Mwana wa Mulungu.<br>2. Abusa aziweto anali osangalala kukumana ndi Yesu ali khanda atamva zomwe angelo anayankhula.<br>3. Ifenso tikuyenera kusangalala ndi kukondwerera kubadwa kwa Yesu. | **Ndime Yowerenga:** ***Luka 2: 25-40***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yesaya 7: 14***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Anthu anakondwa kwambiri chifukwa cha kubadwa kwa khanda Yesu.<br>2. Panali maganizo osiyanasiyana pa za Yesu. Anthu ankayenera kumulandira mwachimwemwe kapena kumukana kwathunthu.<br>3. Ambuye Yesu ndi chipulumutso cha Mulungu, wotumizidwa kudzakhala kuunika kwa dziko lapansi. |
| **MAWU OYAMBA** | Ganizirani momwe amalengezera za kubadwa kwa mwana, mwina ndi makolo ake, makadi kapena zithunzi za khandalo. Pamakhala chisangalalo ndi chimwemwe. Fotokoza kuti Yesu sanali mwana wamba kuti kubadwa kwake alengeze ngati amachitira ndi ana ena! | Pamene mwana wabadwa, pamakhala chisangalalo pakuti anthu akhala akudikira kubadwa kwake miyezi isanu ndi inayi. Fotokozani kuti anthu amene tiphunzira m'Phunziro lino anakhala akudikira moyo wawo wonse kuti akumane ndi mwana uyu amene analonjezedwa – Iwo akuyenera kuti anasangalala kwambiri kuti tsopano awafika! |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Usiku umene Yesu anabadwa, abusa aziweto anali m'tchire kuyang'anira nkhosa zawo. Fotokozani kuti nthawi zambiri kuyang'anira nkhosa usiku ndi kwa bata ndi kopanda chosangalatsa. ***(vesi 8)***<br>2. Koma usiku uwu, mngelo anaonekera kwa iwo ndipo onse anali ndi mantha! *Funsani ophunzira momwe iwo akanamvera mu mtima mwawo.* ***(vesi 9)***<br>3. Mngelo anabwera kudzawawuza za kubadwa kwa Yesu, Mpulumutsi. ***(vesi 11)***<br>4. Kenaka kunaoneka angelo ambiri pamodzi ndi uyu, akuyimba nyimbo zotamanda Mulungu, kukondwerera kubwera kwa Yesu pa dziko lapansi. ***(vesi 13-14)*** *Fotokozani za kukongola kwa maonekedwe ake kumene abusa aziweto anakuona.*<br>5. Angelo aja atachoka, abusa aja anafumulira kupita kuti akaone okha mwanayo. *Kambiranani zomwe iwo ankamva m'mitima mwawo nthawi imeneyi; mwina ankaganiza kuti anali maganizo chabe kapena kuti mngelo sankanena zoona.* ***(vesi 15)***<br>6. Iwo anapeza mwanayo monga m'mene angelo anafotokozera! Iwo anatamanda ndi kukweza Mulungu ndipo anayamba kufotokozera aliyense za Mpulumutsi amene wabadwayu. ***(vesi 16-17)***<br>7. *Kambiranani za kusangalala kwa abusawo pamene anaona khandalo ndi momwe iwo nthawi yomweyo anayambira kuwuza anthu ena za Iye.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Uthenga wa mngelo. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Simeoni anali munthu amene ankamvera Mulungu ndi kumukhulupirira ndi mtima wonse. ***(vesi 25)***<br>2. Mzimu Woyera analonjeza Simeoni kuti asanamwalire adzaona Mesiya amene akhala akumuyembekezera kwa nthawi yayitali. ***(vesi 26)*** *Kambiranani momwe Simeoni ankamvera mu mtima mwake pamene ankakalamba, kudabwa kuti mwina zidzachitika kapena sizidzachitika.*<br>3. Tsiku lina, Simeoni anali m'Nyumba ya Mulungu pamene Mariya ndi Yosefe anafika ndi Yesu ali wakhanda.<br>4. Simeoni anasangalala kwambiri, anatamanda Mulungu, ndi kudalitsa mwanayo. ***(vesi 27-28)***<br>5. Pa ***Luka 2: 31-35*** Simeoni anati Iye adzakhala chimwemwe cha anthu ambiri komanso ambiri adzatsutsana naye. *Fufuzani zomwe Simeoni ankatanthauza pa mawu amenewa.*<br>6. Anna, mneneri, analinso m'Nyumba ya Mulungu nthawi yomweyi. Iye ankakhala m'Nyumbayi nthawi zonse, kupemphera ndi kusala kudya. ***(vesi 36-37)***<br>7. Pamene anaona Yesu ali wakhanda, iye anatamanda Mulungu ndi kuyamba kufotokozera aliyense za Iye. ***(vesi 38)***<br>8. Yesu anapita kwawo ndi makolo ake ndipo anakula, kukhala wanzeru. Mulungu ankakondwera naye. *Fotokozani za kusiyana kwa Yesu ndi ana ena a msinkhu wake.*<br>9. *Kambiranani zomwe Mariya ndi Yosefe ankaganiza ataona zomwe anachita Simeoni ndi Anna ataona mwanayo.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Chipulumutso! |
| **KUKUMBUTSANA** | Pangani posita kapena lembani pa khoma maganizo a momwe iwo analengezera za kubadwa kumeneku. Mulembemo zomwe angelo ananena (onani Vesi Yoloweza) pa maposita anuwo. | Mariya ndi Yosefe anali odzaza ndi chimwemwe ataona chisangalalo ichi chifukwa cha mwana wawo.<br>Phunzirani Vesi Yoloweza ndi kukambirana pa gulu momwe vesiyi ikufotokozera mwachidule Phunziroli. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ndife osangalala ngati abusawa kufotokozera ena nkhani ya Yesu? Kodi mukuganiza kuti kubadwa kwake kunali kosangalatsa monga m'mene iwo anachitira?<br>2. Kodi mumachita chikondwerero cha Khrisimasi pa zifukwa zoyenera? Kodi ndi nthawi ya mphatso ndi maphwando kapena ndi nthawi yokumbukira kubwera kwa Yesu pa dziko lapansi kudzakhala Mpulumutsi? ***(Onani 2 Akorinto 9: 15)*** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Simeoni ndi Anna anali anthu odzipereka kwa Mulungu. Kodi ife timapereka miyoyo yathu kwa Mulungu? Kodi timapemphera kwa Iye ndi kuwerenga Mabaibulo athu?<br>2. Pa Vesi Yoloweza kuti Yesu ndi "Imanueli" kutanthauza kuti "Mulungu ali ndi ife". Ngati ife tikukhulupirira zimenezi, tikuyenera kukhala moyo otani? |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Lachitatu**
- Ophunzira sangatsirize maphunziro awa popanda kuwerenga Baibulo ndipo akuyenera kuwerenga ndime imodzi kapena zambiri.
- Kafunsidwe n'kosiyanasiyana, pena pali mabokosi, pena pali mawu amene akusowa ndi njira zina zambiri.
- Mafunso akonzedwa kuti aziyankhidwa kuchokera m'baibulo la Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero ndi Buku Lopatulika ndi Mawu a Mulungu.
- Cholinga chathu n'chakuti ophunzira onse, kaya akugwiritsa Baibulo la mtundu wanji, azitha kuyankha mafunso.
- Sabata lililonse lili ndi marikisi 20 ndipo pa mwezi pali marikisi 80, ngati munthu wakhonza bwino maphunziro onse.
- Kalasi Lachitatu - Pali marikisi imodzi pa yankho, monga momwe tasonyezera.

**Maphunziro a Kalasi Lachinayi**
- Awa ndi maphunziro ovutirapo kusiyana ndi Maphunziro a Kalasi Lachitatu.
- Muli mafunso ovutirapo ofuna mayankho.
- Marikisi 20 pa sabata ndi marikisi makumi 80 pa mwezi ngati amaliza maphunziro molondola ndiponso mafunso onse ali ndi mayankho ake.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**
Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.
Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**KALASI Lachitatu**
**Ndemanga zina**
"Ntchito yabwino kwambiri! Inu munamvetsa bwino mafunso onse. Ine ndasangalala ndi yankho la funso lotsiriza limene mwaliyankha bwino kwambiri."
"Moni, Yonatani. Ndikuyamika chifukwa cha kulimbikira kwako. Ndi zosangalatsa kwambiri kuti wayesetsa kuyankha mafunso onse. Ine ndalemba mayankho a mafunso ena amene sunayankhe."

**Ndemanga zauzimu**
"Mose anali ndi mavuto ndi ana a Israyeli, koma Mulungu sanamusiye yekha kuti athetse mavutowo."
"Yosefe sanayiwale kuti abambo ake anamuphunzitsa kukonda Mulungu. Iye anakumbukira zimenezi ngakhale anali kutali ndi kwawo."
"Bartimeyu anatsimikiza mtima zofuna kulandira kuchokera kwa Ambuye Yesu. Iye sanakhumudwitsidwe chifukwa tsopano ankatha kuona ndipo anadziwa kuti Ambuye Yesu anali munthu wapadera kwambiri."

**KALASI Lachinayi**
**Ndemanga zina**
"Maphunziro enanso abwino kwambiri. Zikuoneka kuti tsopano ukumvetsa bwino Nkhani za m'Baibulo ndipo ndikukhulupirira kuti wasangalala nazo. Zikomo kwambiri chifukwa chokhala ndi nthawi yokwanira yochita mosamala maphunzirowa. Zikanatheka kuchita mofulumira, choncho ine ndi kuyamika kwambiri."
"Rakele, wayetsetsa ndithu. Ine ndikaona mayankho akowa, zikuonetsa kuti sunamvetse bwino Nkhani za m'Baibulo. Bwanji uwerengenso zimenezi."

**Ndemanga zauzimu**
"Mafanizo nthawi zina amatchedwa nkhani wamba koma zokhala ndi matanthauzo akumwamba kapena ozama. Kodi ungaganizire tanthauzo lozama la fanizo lomwe lili mu Phunziro 3?"
"Stefano anafa imfa yowawa kwambiri, koma iye sanachite mantha ndi imfa, chifukwa ankadziwa kuti anali ndi Mulungu, ndipo ankadziwa kuti akakhala ndi Ambuye Yesu Kumwamba."

## Zoonjezera A – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B7 | Yosefe | **Azondi mu Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-ruler/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-brothers-1/ |
| | | **Benjamini ndi nkhani yoyipa!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-brothers-1/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-reunion/ |
| | | **Kukhululukira ndi nkhani yabwino!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-reunion/ |
| | | **Onse pamodzi mu Aigupto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-reunion/ |
| | | |
| B8 | Alembi a Uthenga Wabwino | **Mateyu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-027-matthew/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-096-jesus-crucifixion/ |
| | | **Marko** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-prison/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-capernaum/ |
| | | **Luka** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-tempted/ |
| | | **Yohane** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-104-appearance-thomas/ |

## Zoonjezera A – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| B7 | Moyo wa Yosefe | **Mayesero a chinyamata chake** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-prison/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-prison-dreams/ |
| | | **Malo ake okwezedwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-pharaoh-dreams/ |
| | | **Mtima wake wosamalira** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-ruler/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-brothers-1/ |
| | | **Kukhululukira kwake kwathunthu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joseph-reunion/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/joseph-jacob/ |
| | | |
| B8 | Zoyenera Kuchita | **Akhristu kusonkhana pamodzi** |
| | | https://freebibleimages.org/illustrations/pentecost/ |
| | | https://freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/ |
| | | **Ubatizo wa Chikhristu** |
| | | https://freebibleimages.org/illustrations/gnpi-106-great-commission/ |
| | | https://freebibleimages.org/illustrations/gnpi-013-jesus-baptism/ |
| | | **Mgonero wa Ambuye** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/last-supper-jesus/ |
| | | **Kukula kwa Mkhristu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-last-days/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/redemption-story/ |

| Zoonjezera A – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m’Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m’Chithunzi** |
| **B9** | **Mose** | **Mwana mu ndengu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses1/ |
| | | **Cholakwa chake chachikulu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses1/ |
| | | **Chitsamba choyaka moto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses2/ |
| | | **Kubweretsa uthenga wa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses2/ |
| | | |
| **B10** | **Mose** | **Mwanawankhosa wa Paskha** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses2/ |
| | | **Nyanja Yofiira** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-moses3/ |
| | | **Ulendo wovuta** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-food-water/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-amalekites/ |
| | | **Njoka yamkuwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-serpent/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-017-nicodemus/ |

| Zoonjezera A – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m’Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m’Chithunzi** |
| **B9** | **Mose** | **Kalonga** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/baby-moses/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-prince/ |
| | | **M’busa wa ziweto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-burning-bush/ |
| | | **Mtsogoleri** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-pharaoh/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-plagues-1/ |
| | | **Mpulumutsi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-plagues-2/ |
| | | |
| **B10** | **Mose** | **Kuwoloka Nyanja Yofiira** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-red-sea/ |
| | | **Pa Phiri la Sinai** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-sinai/ |
| | | **Kutuluka m’moto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-golden-calf/ |
| | | **M’chipululu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-serpent/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-017-nicodemus/ |

| Zoonjezera A – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| B11 | Mose | **Kukumana ndi Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-sinai/ |
| | | **Kudziwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-sinai/ |
| | | **Kumvera Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-golden-calf/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-074-rich-ruler/ |
| | | **Kukhumudwitsa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-golden-calf/ |
| | | |
| B12 | Nkhani ya Khrisimasi | **Malonjezo a Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/prophecies-birth-jesus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-names-jesus/ |
| | | **Kudabwa kwa Mariya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-003-birth-announcement/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/ |
| | | **Kubadwa kwa Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ed-jesus-birth/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-007-birth-jesus/ |
| | | **Uthenga wa mngelo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-christmas-story/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-shepherds/ |

| Zoonjezera A – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
| B11 | Mose | **"Mulungu m'modzi"** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-sinai/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-golden-calf/ |
| | | **"Njira ya Mulungu"** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moody-moses-commandments/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-066-stooped-woman/ |
| | | **"Mulungu akhale woyamba"** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moody-moses-commandments/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-rich-man/ |
| | | **"Mawu a Mulungu"** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/feeding-5000/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-withered-hand/ |
| | | |
| B12 | Nkhani ya Khrisimasi | **Mwana wamwamuna wabadwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/ |
| | | **Kulengeza za Mpulumutsi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-shepherds/ |
| | | **Kupembedza Ambuye** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-wisemen/ |
| | | **Chipulumutso!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/simeon-anna/ |

© Bible Educational Services 2020

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 08/2024
(Chichewa)